

# UMODZI WA CHIYANJANO



Wokondwa kukhala nawo mwayi wobwera mu Kukhalapo Kwanu ndi kudzakomana ndi Inu. Ndipo, O Mulungu, mulole ife tikhale nacho chiyanjano usikuuno kuzungulira pa Mawu olembedwa. Mulole Mzimu Woyera udzoze zonse zomwe zachitidwa kapena kunenedwa. Kwa ulemerero wa Mulungu ife tikupempha izi, mu Dzina la Yesu. Amen.

Inu mukhale pansi.

<sup>2</sup> Iwo anatsala pang'ono kundidzidzimutsa ine. Ine ndinali kuyang'ana pansi apa pa m'bale wamng'ono wachi Arkansas wochokera kutali komwe mu dziko lalikulu la Arkansas. Ndipo kodi inu mukuchita chiani kuno mu dziko lozizira lino nanga?

<sup>3</sup> Chabwino, kulikonse kumene ine ndimapita, ine ndimakomana ndi anthu ochokera ku Arkansas. Awo anali amodzi a malo anga oyamba kuti ndipiteko nditachoka ku Saint Louis, kumene ife tinali ku Nyumba yoyankhuliramo ya Keil, ndipo ndinapita uko ku Arkansas. Ndipo ine sindimawaiwala konse anthu awo, momwe iwo amadzera. O, basi, uko kunali anthu twente-eyiti sauzande; nyuzipepala inatero, mu Jonesboro. Ndipo mzindawo uli pafupi eyiti kapena teni sauzande, ine ndikuganiza, chiwerengero. Kwa mailosi sate kuzungulira mzindawo, kunalibe zina; manyumba onse aku farmu anali atatengedwa, ndi mahema atamangidwa ndi zinthu, ndi anthu akukhala umo, pansi pa zimagalimoto za-zakale. Ndipo anthu, ikuvumba. . . Iyo imakhoza kumavumba, anthu atagwirizira zidutswa zazing'ono za malona ndi nyuzipepala pa anthu odwala awo, kumangoyembekezera kuti iwo apemphereredwe. Izo sizinapange kusiyana kulikonse ngati abwera sabata ino kapena sabata ya mawa. Paliponse pomwe izo zinali, izo zikanakhala zabwino. Mukuona?

<sup>4</sup> Ine ndikukumbukira kumusi ku Corning. Inu mumakhala pafupi ndi kumeneko, sichoncho inu? Corning. Inu mukuoneka. . . Ine ndinawona chinachake uko chomwe ine ndikulingalira kuti mwinamwake Dwight Moody, kapena Sankey, kapena ena a iwo anachiwona mu tsiku lawo.

<sup>5</sup> Ine ndinali kutali komwe mu chipululu, ndinali nditadzizatula ndipo ndinali kuseri uko ndikupemphera, ndekha, usanayambike msonkhano. Ine ndimakhoza kuwawona anthu akubwera kuchokera mnjira zafumbi izo, akupita ku msonkhano uko, cha madzulo. Ine ndinazindikira madona aang'ono, madona aang'ono okongola, osapitirira usinkhu wa zaka sikisitini, eyiti, atanyamula nsapato zawo ndi masitonkeni m'nhwapa mwawo. Asanafike uko, iwo amakhala pansi, kupukuta fumbi pa mapazi awo, ndi kuvala zammiyendo zawo

ndi nsapato zawo. Iwo anali ndi peyala imodzi yokha, ndipo iyo imayenera kuti izingokhalapo. Koma iwo ankawakonda kwenikweni Ambuye.

<sup>6</sup> Zina za zozizwitsa zopambana zomwe ine ndinayamba ndaziwonapo zitachitidwa mu Amereka zinachitidwa uko. Ndipo ine ndikufuna kuti ndidzabwererenso ku Arkansas, lina la masiku amenewa, kudzangokhala ndi nthawi yachikale ya chiyanjano pa Mawu ndi anthu a Mulungu.

<sup>7</sup> Tsopano, ife tangolawirira pang’ono, usikuuno, ndipo kotero ife tikuti tiwerenge Mawu ena a Mulungu Amuyaya, mwa chizolowezi. Ndipo ine ndikufuna kuti . . .

<sup>8</sup> Nditi, ine ndikukhulupirira iwo anati, kuno, ife tinali . . . Inu munali mutalengeza kale za kadzutsa wa azitumiki uja, ndi zina zotero? [Wina ati, “Eya.”—Mkonzi.] Eya. Chabwino. Zonse ziri bwino, ndiye.

<sup>9</sup> Ife tikufuna kuti tiwerenge usikuuno kuchokera mu Bukhu la Genesis. Ndipo ine ndikufuna kuti inu muzimvetsera pamene ife tikuwerenga kuchokera pa mutu wa 11 ndi ndime ya 5.

*Ndipo Yehova anatsika kuti adzawuwone mzindawo  
ndi nsanja, yomwe ana a anthu anali atazimanga.*

*Ndipo Yehova anati, Taonani, anthuwa ali amodzi, . . .*

<sup>10</sup> Ine ndikufuna kuti ndiyankhule, usikuuno, pa *Umodzi Wa Chiyanjano*, tsopano, pamene ife tikupita molunjika mu Mawu, kwa chilimbikitso ichi. Ndipo tsopano ine . . . Ndi zodabwitsa kwambiri, kuti uganize izo, momwe kuti anthu amene anawawona apa anali amodzi.

<sup>11</sup> Ndipo, inu mukudziwa, ndilo dongosolo la Mulungu, Mulungu amafuna anthu kuti akhale amodzi. Ndipo ndi chachilendo kuti uchiganizire, koma Mdierekezi amayesera kuti ayike dongosolo lake kuti likhalepo ndi kuwapanga anthu kukhala amodzi pansi pa dongosolo lake. Tsopano, Mulungu ali nalo dongosolo, ndipo Mdierekezi ali nalo dongosolo. Ndiyeno Mdierekezi akuyesera kuwatengera anthu onse pansi pa dongosolo lake, pamene Mulungu akuyesera kuti awatengere anthu kuti akhale amodzi pansi pa dongosolo Lake.

<sup>12</sup> Kotero ilipo mizimu iwiri yaikulu mu dziko, umodzi wa iwo ndi Mdierekezi, winawo ndi Mulungu. Mdierekezi ali nawo atumiki, Mulungu ali nawo atumiki, ndipo ife tiri pa ufulu woti tipange kusankha kwathu. Komwe tingadzipererekereko ifeeni, ndi komwe tiri antchito ake. Koma ngati inu mungazindikire monga . . .

<sup>13</sup> Ine ndinali kulalikira Lamlungu lapitali za ludzu lomwe liri mwa anthu, munthu. Mulungu anamupanga munthu kuti azichita ludzu, koma kuti azichitira ludzu kwa Iye. Ndicho chifukwa ludzu linayikidwa mwa munthu.

<sup>14</sup> Koma Mdierekezi amabwerapo ndi kuzipotoza izo, ndi kumawapangitsa anthu kuti azichitira ludzu kwa iye, ndi zinthu za mdziko. Baibulo linati, “Ngati inu mulikonda dziko kapena zinthu za mdziko, chikondi cha Atate sichiri mwa inu.” Ndiye, inu mukuona Mdierekezi amapotoza. Iye sangakhoze kulenga chirichonse, koma iye akhoza kupotoza zomwe Mulungu wazilenga kale. Mdierekezi si mlengi. Iye ndi wongopotoza wa cholengedwa chapachiyambi. Ndipo kodi tchimo ndi chiyani? Ndi chilungamo chopotozedwa.

Ndi angati akumvetsa izo? Mwaona? Chabwino. Ine ndimangodabwa.

<sup>15</sup> Ndine Wakummwera, ndipo ife tangokhala ozolowera pang’ono pa ku kuvomereza kochulukirapo kuposa uku. Ndipo anthu—Akumpoto ndi odzigwira. Ndi—ndipo ine ndakhala ndiri Kummwera motalika kwambiri mpaka inu muyenera kuti mungozolowera njira zanga Zakummwera, kapena ine ku njira yanu ya chi Yankee.

<sup>16</sup> Koma ine ndikufuna kuti inu mudziwe, ife tinapambana nkondo. Eya. Ife tiribe kutsutsana pa izo. Alipo Wakummwera mmodzi ali moyo, ndipo palibe ma Yankee, kotero ife tinapambana nkondo. Ine ndimaganiza chinali chokhudza kwambiri pamene wachi Yankee wamng’ono uja anali kufa, ngakhale, ndipo Wakummwera anamutumizira iye telegramu ndipo anati, “Mulungu akudalitse iwe, Yankee. Ine ndikuyembekeza kudzakuwona iwe kachiwiri, posachedwa kwambiri.” Ndizo, chifukwa iwo samaganiza izo pachiyambi, inu mukuona, ndi kungozilola izo zipite? Koma ine ndikanakonda kuti ndinene izo, kuti alipo kokha... Izo zinatengera madanga a moyo, kuti apambane nkondo, koma ife potsiriza tinakwanitsa izo. Mukuona? Chabwino. Koma ilipo nthawi yaikulu ikudza.

<sup>17</sup> Ndipo tsopano poyankhula za m—mdani, za momwe iye amapotozera chilungamo kukhala kusalungama. Tsopano, poti, ndife gulu losanganikirana, tonse amuna ndi akazi, pafupi tonse ndi achikulire, kotero ine ndikutsimikiza inu mumvetsa. Inu mumamvetsera kwa dotolo wanu, ndipo ndine m’bale wanu. Ndi chovomerezeka, ndi chololedwa, ndi chaumulungu, kuti mwamuna adzitengere yekha mkazi, ndi kumakhala naye mkazi uyu. Koma mkazi wina chikhoza kukhala chinthu chomwecho kwa iye, koma icho chikanati chikhale imfa kuti amugwire iye. Uko ndiko kusiyanako, chilungamo chopotozedwa. Ndi momwe tchimo lirilonse liri, ndi chilungamo chopotozedwa.

<sup>18</sup> Mulungu anakupangani inu kuti muzimuchitira Iye ludzu, ndipo Mulungu anaupanga Mpingo kuti ukhale waumodzi pansu pa ulamuliro Wake. Koma Mdierekezi amawapanga iwo aumodzi pansu pa ulamuliro wake.

<sup>19</sup> Ndipo tsopano ngati inu mungazindikire mu chipembedzo Chachimuhamadi, zinthu zina, ngati ife tikanangoti titenge nthawi. Zinthu zomwe ziri, momwe izo zapotozedwera! Mu chipembedzo cha Chimuhamadi, chomwe ine ndinali nawo mwayi wokayendera dzikolo pafupi ndi manda a Muhamadi, ndipo pa manda ake pakhala pali kavalo woyera wakhala ataima apo kwa zaka zikwi ziwiri. Maora anai aliwonse, ine ndikuganiza iwo ali, iwo amasinthu mulonda, ndi kavalo woyera, ataikidwa chisyalalo, ndipo akuyembekezera chiukitsiro cha Muhamadi. Ndipo iwo amanena kuti iye adzauka kwa akufa, adzakwera pa kavalo, ndi kudzaligonjetsa dziko lonse.

<sup>20</sup> Ndiye, inu mukuona, iwo akuyembekezera kuti mgonjetsi abwere, atakwera pa kavalo woyera, ndi momwe izo ziri zopotozedwera kuchokera ku Malemba. Chifukwa, “Yesu akudza, atakwera pa kavalo woyera, chovala Chake chitaviikidwa mmagazi; Dzina Lake, Mawu a Mulungu.” Koma, inu mukuona, Mdierekezi anatengera lingaliro ilo ndipo analipotozera ilo kwa Muhamadi. Koma, moonadi, Yesu adzadzpa pa kavalo woyera. Baibulo limanena kuti Iye adzatero.

<sup>21</sup> Ndipo inu mukhoza kulowa mu kagulu kabodza kalikonse kamene inu mukukafuna ndipo inu nkuwonamo zophiphiritsa zambiri zazikulu za Chikhristu choona.

<sup>22</sup> Tsopano, mu nsanja ya Babeloni, ngati inu mungazindikire nsanja imeneyo, iyo inali Babeloni woyamba; zomwe ine nditi ndiziyankhule mtsogolomo sabata ino, Ambuye akalola. Babeloni, mzinda womwe, unafanizitsidwa ndi wa Kumwamba. Ndipo mmenemo iwo ali ndi mtsinje wa Firate ukuyenderera kuchokera cha ku mpandowachifumu ndi munda, munda wammalere. Ndipo ndizo zokonzedwa mofanizitsa Kumwamba, pakuti Mtsinje wa Moyo, Mpand-...umayenderera cha ku Mpandowachifufumu wa Mulungu. Ndipo inu mukuona kupambana kumene munthu anali kuchita, anali akupanga ndondomeko, yosokonezedwa.

<sup>23</sup> Ndiyeno, mu chinthu chachikulu ichi, iwo anali naye munthu dzina lake Nimrodi. Ndipo Nimrodi anali kuyibweretsa mizinda yonse ndi fuko pansi pa ulamuliro umodzi wawukulu, kusonyeza kuti ndi lingaliro lopangidwa ndi munthu, ndondomeko yokhayo.

<sup>24</sup> Koma Mpingo wa Mulungu ndi wolumikizidwa pansi pa Mulungu. Munthu alibe kanthu kochita ndi Iwo. Iwo ndi woyanjana pansi pa Mulungu.

<sup>25</sup> Ndipo Babeloni uyu, yemwe anali chiyambi cha...Mu chilengedwe, mu Genesis, ife tikupeza kuti izo zafika mpaka mu Chivumbulutso, ndipo izo zimayankhula za dziko lake lazamipingo mu masiku otsiriza, lomwe liri tsopano, potsiriza adzalumikizana pansi pa wotsutsakhristu, chipembedzo chopangidwa ndi anthu.

26 Koma ndine wothokoza ponena kuti Mpingo wa Mulungu udzakhala woyanjana, nawonso, pansi pa Mutu umodzi, Mulungu.

27 Koma zipembedzo zopangidwa ndi anthu zonse zidzabwera mu chipembedzo chotsutsakhristu ichi. Padzakhala mawonekedwe awiri a iwo. Mawonekedwe amodzi adzabwera kuchokera kwa Roma, omwe ati adzakhale chirombo. Ndipo pali chifano cha kwa chirombo, chomwe chiti chidzakhale mutu wazamipingo wa mpingo wa Chiprotestanti, atausanjikika ngati fano la kwa chirombo, pansi pa dziko lachipembedzo. Ndipo izo zonse zidzadza pansi pa ulamuliro umodzi waukulu, ndipo wotsutsakhristu adzakhala yemwe ati adzaikidwe pa mpandowachifumu nakhalapo. *Anti*, “kutsutsa,” pafupifupi wofanana ngati, komabe c—c—chiphunzitsa chake si chochokera ku Malemba. Malemba okwanira ozipangitsa izo kumawoneka ngati kuti nzolondola, koma izo zidzakhala ziri zolakwika.

28 Ndipo ine ndikudziwa inu—inu mukuti, “M’bale Branham, inu mukulozera kwa Roma tsopano.” Ndizo ndendende. Ndipo osati kokha Roma, koma Chiprotestanti, nachonso. Ndendende. Baibulo linanena chomwecho.

29 Koma ndi inu apo, Mdierekezi kuwalumikizitsa anthu pansi pa mutu umodzi, mutu umodzi wa zamipingo, munthu pansi pano. Baibulo linati, “Iye akanati azidzakhala mu kachisi wa Mulungu, kumasonyeza kuti iye ali Mulungu.” Ndi momwe iye ati azidzavalira nduwira ya patatu, ndi zinthu zonse izi zomwe iye akanati adzachite, “Wolowa mmalo wa—wa kumwamba, dziko lapansi, ndi purigatorio.” Ndipo pansi pa uyu padzakhala pali f—fano kwa iye, komwe ena onse awo ati adzalumikizane limodzi.

30 Koma Mpingo wa Mulungu wamoyo udzalumikizana pansi pa mphamvu ya Mulungu ndi kuyang’anira kwa Mzimu Woyera. Mpingo wa Mulungu udzalumikizidwa. O, kodi sindinu okondwa?

31 Mu ora la mdima ili, pamene chirichonse chikutsekeka, anthu sali kusamala. Iwo sali. Zikuwoneka ngati mitima yawo ikutalikira talikira kutali ndi Mulungu. Dziko likuzizira zizira, ndi kusayanjanitsika, chifukwa mitu yaikulu ya zamipingo iyi ikupangika.

32 Mu Russia, Russia akuyesera kuti aliyanjantse dzikoli pansi pa chikominisi, Russia. Mdierekezi yemwe akulamulira Russia akuyesera kuti aliyanjantse dziko lonse pa chikominisi. Iwo sadzakhoza konse kuzichita izo.

33 Ndiyeno U.N., United Nations, ikuyesera kuti iwayanjantse iwo pansi pa chiyanjano cha mphamvu ya apolisi, kachitidwe kena kopangidwa ndi anthu. Izo sizidzagwira konse ntchito. Izo sizingakhoze. Koma iwo onse akuyesera kutero.

<sup>34</sup> Ndipo mundilole ine ndinene izi ndi kulemekeza, koma molingana ndi Mawu a Mulungu, kuti fuko lirilonse lero likulamuliridwa ndi Mdierekezi. Baibulo linanena chomwecho. Satana anawasonyeza Ambuye wathu maufumu a mdziko, ndipo iye anati, “Awa onse ndi anga, kuti ndizichita nawo chirichonse chimene ine ndikufuna kuchita. Ndipo ngati Iwe uti undipembedze ine, ine ndiwapereka iwo onse kwa Iwe.

<sup>35</sup> Ndipo Yesu ankadziwa kuti Iye akanati adzakhale wowalandira iwo mu Zakachikwi, kotero Iye anati, “Pita kumbuyo Kwanga iwe, Satana.”

<sup>36</sup> Ngati dziko likanakhala likuyendetsedwa ndi Khristu, ife tikanaujika zida zathu ndipo sipakanadzakhala chipolopolo china chikanawomberedwa. Ife sibwenzi tiri nawo ntchito iliyonse ma sputnik ndi mabomba a haidirojeni, kuti aziphulitsa anthu. Pamene Khristu adzatenga ulamuliro wa dziko lino, monga “Mfumu ya mafumu ndi Mbuye wa ambuye,” anthu adzakhala olumikizidwira kwa Iye, pansu pa ulamuliro umodzi waukulu. Iyo idzakhala nthawiyo!

<sup>37</sup> Mafuko onse akufuna kuti anthu akhale amodzi. Germany inkaganiza kuti iwo onse amayenera kuti akhale achi German. Russia akuganiza kuti iwo onse akuyenera kuti akhale achi Russia. A dziko lakumadzulo akuganiza kuti iwo onse ayenera kuti azibwera kuno. Ndipo iwo akufuna kuti iwo aziyankhula chinenero chimodzi, basi monga iwo ankachitira mu Babeloni. Mulungu anati, “Iwo ali achinenero chimodzi.” Ndipo iye akuwafuna iwo onse kuti aziyankhula chinenero chimodzi. Iwo akufuna kuti iwo onse akhale munthu mmodzi woyanjanitsidwa, koma izo sizidzachitika nkomwe pansu pa ulamuliro wa munthu.

<sup>38</sup> Koma ine ndinene izi, kuti palikudza nthawi pamene mafuko onse ati adzalumikizane palimodzi pansu pa Mfumu imodzi, ndipo uyo adzakhala ali Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu. Ndipo iwo azidzayankhula chinenero chimodzi. Iwo adzakhala amodzi mu mtima ndi amodzi mu cholinga. Daniele anawona mapeto, pamene Mwala unadubuzidwa kuchokera m’phiri, popanda dzanja, ndipo Iwo unagudubuzikira mu maufumu a mdziko ndi kuwapera iwo, ndipo iwo anakhala ngati mungu pa dwale, mankhusu omwe mphepo inawaulusa. Koma Mwala unaphimba dziko lapansi lonse. Mwala umenewo ndiwo Khristu. Kudzakhala kuli nthawi yina kuti kudzakhale kuli fuko limodzi, anthu amodzi, mbendera imodzi: mtanda wakale wokhukhuluzidwa. Matamando akhale kwa Mulungu wamoyo!

Ziyembekezo zanga sizinamangidwe penanso  
 Koma Mwazi wa Yesu ndi chilungamo;  
 Pamene ponse pozungulira solo yanga  
 ikuchoka,  
 Ndiye Iye ali chiyembekezo changa chonse ndi  
 pokhazikika

Pakuti pa Khristu, Thanthwe lolimba, ine  
ndaima;  
Maziko ena onse ndi mchenga wotitimiritsa.

<sup>39</sup> Maziko ena onse, mipingo, zipembedzo, mafuko, U.N., chirichonse chomwe chingakhale chiri, izo zonse ndi mchenga wotitimira, ziyenera kufika pa mapeto.

<sup>40</sup> Ine ndinali nawo mwayi woyima mu Roma, kumene Kaisara wamkulu yemwe anayesera kuti aliyanjaniitse dziko lonse pansi pa ufumu wa Chiroma. Ndipo, lero, inu muyenera kuti mukumbe mapazi twente pansi, kuti mupeze mabwinja a mzinda umenewo.

<sup>41</sup> Ine ndinaina ku Igupto, kumena mafarao aakulu omwe ankayesera kuti aliyanjaniitse dziko pansi pa Igupto, ndipo inu mumakumba mapazi twente ndi sate, kuti mupeze mabwinja a mzinda. “Pakuti kuno ife tiribe mzinda wopitirira,” limatero Baibulo, “koma ife tikufunafuna Wina ukudzawo.”

<sup>42</sup> Si kale litali, pamene ine nthawiyina ndinapita ku malo pamene ine ndinali mnyamata wamng’ono. Ine ndinawona mtengo waukulu, kumene ine ndinkakonda kupita ndi kukakhala pansi pa mtengo umenewo. Ine ndinati, “Pamene ine ndidzakhala bambo wachikulire, ine ndizidzabweranso ndi kudzakhala pansi pa mtengo winawake uwu, ndipo ine ndizidzayang’ana mmwamba mu nthambi zake. Ine ndizidzasilira kukongola kwake, monga ine ndiriri lero, ndiri mnyamata wa thwelofu.” Palibe kanthu katsalira ka mtengo umenewo koma chitsa. Chifukwa? Kulibe kanthu kuno komwe kangakhoze kupitirira. Izo ziyenera kutha.

<sup>43</sup> Ndipo chinthu chachivundi chirichonse chimayankhula za chachisavundi Icho chikudzacho, chifukwa chirichonse chimene ife tikuchiwona ndi kachitidwe kopotozedwa ka chinachake chomwe chiri chenicheni.

<sup>44</sup> Ine ndimawakwatitsa awiri, ndi kuona msungwana wamng’ono wokondeka mu zakhumi zake zamanyazi, mnyamata ali ndi mapewa ake mmbuyo, ataima monga iwo aliri, amodzi, ndipo mitima yawo ikugundira limodzi. Ine ndimaganiza, “Kodi icho si chithunzi chokongola kwambiri choti chidzaonongedwe konse ndi imfa?” Koma ndi zaka pang’ono zokha mpaka tsitsi lawo limasanduka la imvi, mapewa amagwa, ndi kubwerera ku fumbi iwo amapita. Nchiani icho? Ndi chithunzi, pamene iwo akuima apo, kuti liripo Dziko kutsidya kwa Mtsinje, kumene chisonyezo chirichonse cha imfa chimachotsedwako. Uko, mwachisavundi, tidzaima mofanana Naye, dzuwa ndi nyenyezi kuwala moziposa.

<sup>45</sup> Nyenyezi yaikulu yammawa ija siyinataye kukongola kwake kulikonse kuyambira pamene Ambuye anaiwuzira iyo kuchokera mmanja Mwake ndi kuyipachika iyo mu kanjira kake, ndipo taonani chomwe zaka zapang’ono zimachita kwa

ife. Koma kodi Iye ananena chiani mu Lemba? Iye anati, “Iwo amene atembenezira ochuluka ku chilungamo adzawala kuposa nyenyezi.” “Kotero ife tikufunafuna Mzinda Womwe Mmisiri wake ndi Wowupanga Wake ndi Mulungu.”

<sup>46</sup> Inu mutatha kuwona chinachake chachikulu ichi chimene ine ndikuyesera kuti ndimangirepo malingaliro anu, kwa nkhanayi, ine ndikuyesera kuti ndikusonyezeni inu kunoko kuti kuli—kugwira ntchito kwa mdani. Ndipo kugwira ntchito kwa mdani, mwa mzimu wopotozedwa, kuli kuyesera kumachita icho chomwe Mzimu wa Khristu ukuyesera kuti uchite. Mdani akuyesera, monga zovomereza ndi zotsutsa, kuti aliyanjantitse dziko lonse pansu pa mutu umodzi waukulu. Dziko likuchita izo; Russia, U.N. Ndipo tsopano mudirole ine ndipite patsogolo pang’ono pokha. Ndipo mpingo ukuyesera kuti uchite izo, pansu pa kakonzedwe kopangidwa ndi munthu. Izo sizidzagwira konse ntchito. Sindiyo purogramu ya Mulungu. Ine ndikhoza kutsimikizira izo mwa Mawu Ake.

<sup>47</sup> Koma, inu mukudziwa, Mulungu anakupangani inu munthu, kuti akupangeni inu muzisilira mutakhala mwa njira iyo, kotero kuti Iye akanati akudzazeni inu ndi ubwino Wake. Tsopano, ngati . . . Munthu ayenera kuti azikhala wodzaza ndi chinachake. Ndiko kulondola.

<sup>48</sup> Ino ndi nthawi yosankha. Iwe sungangoima pakatikati mopitiriranso. Inu mukhoza kuchokapo uthengawu usanathe, koma inu simungakhoze kutuluka pa khomo ilo munthu yemweyo yemwe inu munalowa muno. Ndiko kulondola. Inu mudutsa chiundo icho, usikuuno, mwina munthu wabwinoko kapena m—munthu woipa kwambiri kuposa momwe inu munaliri pamene inu mumalowa. Inu simungakhoze kuziletsa izo. Izo ziri kwa inu kuti mupange kudzisankhira. Tsopano, zindikirani, ndi nthawi yosankha. Inu simungakhoze kukhala pakatikati. Ndi nthawi yosankha. “Inu muyenera kudzisankhira lero yemwe muti muzimutumikira.” Ndipo Mdierekezi wapereka zinthu zochuluka, zokongola, zomwe inu mungakhoze kuzisankha ngati inu mukufuna kutero. Inu simungakhoze kutsala momwe inu muliri. Chifukwa, inu muyenera kuti mukhale . . . ngati muli opanda kanthu.

<sup>49</sup> Tsopano, ine ndikukhumba ichi chikanatsala pakati pathu. Ndipo Ambuye wabwino wa Kumwamba akudziwa kuti ine sindiri kunena izi kuti ndikhale wosiyana. Koma ine ndikungonena izi kuti ndisonyeze Choonadi. Ndipo alaliki athu aakulu omwe akuwoloka dziko lero . . .

<sup>50</sup> Ndipo si kale litali, ine ndinali nawo mwayi wa kukhala pa kadzutsa ndi Billy Graham wotchuka uyu, yemwe ine ndikukhulupirira ndi wantchito wa Mulungu, akupita kudutsa fuko, kuwaitanira iwo kwa Khristu, kuliitanira dziko kwa Khristu ndi ku kulapa. Ndipo ine ndinamumva iye akuti, pamaso



pa gulu la alaliki, pamene iye ankanyamula Baibulo, monga *chonchi*, ndipo iye anati, “Ichi ndi—chitsanzo.” Iye anati, “Paulo ankapita mu mzinda ndipo ankapanga wontembenuka. Iye ankabwerera chaka chinacho ndipo iye anali ndi otembenuzidwa sate.” Iye anati, “Ine ndimapita mu mzinda ndi kukakhala nawo otembenuzidwa twente sauzande. Ine ndikabwerera mu chaka ndipo sindimakhala nawo twente.” O, momwe ine ndinkafunira kuti ndinene chinachake! Koma uwo unali msonkhano wake.

<sup>51</sup> Billy Graham, ndi uthenga wake, ali kuwauza anthu kuti alape ndi kuti atembenuke kuchokera ku tchimo. Ndipo iwo ndi Uthenga wofunikira. Ndipo Mulungu wamusankha Billy Graham kuti azichita izo. Palibe wina aliyense angakhoze kuchita izo monga momwe iye wachitira, chifukwa iye akuwatsatira Ambuye. Iye ali mu mzimu wa Yohane, chomwe, kusanachitike kudza koyamba kwa Khristu, ankapita konse ndipo ankalalikira kulapa ndipo sanachite zozizwitsa, koma iye ankalalikira ndipo anakondoweza makamu ndipo ankawapangitsa iwo kukhala okonzekera uthenga wotsatira umabwerawo.

<sup>52</sup> Koma, lero, monga Billy Graham, m’bale wathu wokonedwa, pamene iye akumakhala ndi anthu kuti adziike okha kunja kwa tchimo, iye alibe uthenga wodzazitsamo kachiwiri. Ndilo lomwe liri vuto: inu mwazisiya izo kunja.

<sup>53</sup> Koma munirole ine modzichepetsa ndiyankhule kwa inu, ngati m’bale wanu. Baibulo linati, “Pamene mzimu woipa uchoka mwa munthu, iwo umakayenda ku malo ouma.” Mwa kuyankhula kwina, iwo ukupitapita, kulikonseko, kuyesera kuti upeze pokapuma. Mzimu sumakhala woyipa kwambiri mpaka iwo utamupeza winawake yemwe ungati uziyankhula kupyoleramo kapena kumakhala moyo kupyoleramo.

<sup>54</sup> Basi posachedwapa, ine ndimakhoza kuumverera mzimu mu msonkhano. Ndipo inu nonse omwe mukumatumiza makalata anu, mwa kupepesa kwa usiku woyamba kapena wachiwiri, pokhulupirira kuti zinali mtundu wina wa zammutu zongokonzedwa, ndipo tsopano inu mwakhutitsidwa. Ndithudi, ine ndakukhululukirani inu. Mulungu, watero, nayenso. Ndipo Ambuye akudalitseni inu. Ndithudi.

<sup>55</sup> Tsopano, pamene msonkhano ukupitirira, mzimu woipa mu msonkhano, mzimu uwo umakhala wosawononga mpaka iwo utamupeza winawake yemwe iwo ungamagwiriremo ntchito. Ndiye pamene iwo ungagwiremo ntchito, iwo ndithudi ungachite zowononga, chifukwa iwo ndi mzimu woipa.

<sup>56</sup> Ndipo Mzimu Woyera uli muno, ukuyesera kuti umupeze winawake kuti uzigwiriramo ntchito. Ndipo pamene Iwo umupeza wina kuti uzigwiriramo ntchito, Iwo ukhoza kuchita zabwino.

<sup>57</sup> Mukuiwona mizimu iwiriyo, zolinga zawo, chochifuna? Taonani momwe izo ziriri. Penyani ntchito zawo. Penyani zipatso zawo, ndiye inu mukhoza kuwona mzimu womwe uli pa inu. Inu mumachititsidwa ndi mzimu. Ngati inu mulibe mzimu, ndinu wakufa. Ndipo ngati inu muli ndi mzimu, iwo umachititsa moyo wanu.

<sup>58</sup> Ndipo ngati moyo wanu ukubala chipatso cha Mkhristu, ndi Mzimu wa Mkhristu. Tsopano, inu mukhoza kudzazidwa.

<sup>59</sup> Tsopano upenyeni mzimu woipa uwu. “Pamene iwo utulukamo, iwo umakayenda mu malo owuma, kusakasaka malo oti ukapeze popuma.” Baibulo linati, “Iwo sumakhoza kuwapeza iwo, kotero iwo umati, ‘Ine ndibwereranso kumene ine ndinatulukako.’” Iwo umabwereranso kwa munthu uyu yemwe iwo nthawiyina unalimo, ndipo iwo umakaipeza nyumba yonse itasesedwa, itatsukidwa, itayeretsedwa, kutsutidwa konse kutachokamo. O, wokhulupirira wokondwa weniweni basi, koma mulibemo kanthu. “Ndipo iwo umati, ‘Bwerani muno,’ mizimu ina seveni yoipa kuposa momwe iye analiri.” Chonde mungayesere kumvetsa izi? Baibulo linati izo Nzoona. Yesu anati izo Nzoona. “Ndipo iwo umabwereranso ku nyumba yake.”

<sup>60</sup> Munthu yemwe wamuvomereza Khristu kuti ndi Mpulumutsi wake, wachotsa kuipa kwake, wasiya kumwa kwake, wasiya kusuta kwake, kunama kwake, kuba kwake. Iye wakhala woyeretsedwa, watsukidwa. Nyumba yake yonse yasesedwa. Iye akumverera kumasuka. “Kotero iwo umabwerera ndipo amadzaipeza nyumba ija. Ndiye iwo umapita ndi kukapeza mizimu ina seveni yoipa kuposa momwe iye analiri, ndipo imabwera mwa munthu uyu.” Ndipo Baibulo linanena, kuti, “Chikhalidwe chotsiriza cha munthuyo chimakhala kaseveni kuipa kwake kuposa momwe zinaliri poyamba.”

<sup>61</sup> Tsopano nchiani chachitika? Mlaliki akabwera nadutsako, amalalikira kulapa, ndipo inu mumatsukidwa ku tchimo lanu. Ndiyeno pamene inu mwatsukidwa, Mdierekezi amachoka kwa inu. Inu mumatenga zinthu zanu kukazibweza, zomwe inu munaziba. Inu mumapita, mumakalapa zolakwitsa zanu kwa akazi anu kapena amuna anu. Inu mumatsukidwa kwenikweni. Ndiyeno, chinthu chake ndi ichi, iwe wangotsukidwa, ndipo wadzipanga kukhala chandamale chabwino kwa Mdierekezi.

<sup>62</sup> Tsopano, “Anthu atakhulupirira kale ndipo atabatizidwa, iwo anadzazidwa ndi Mzimu Woyera.” Ndipo ndiyo ndondomeko Yaumulungu ya Mulungu. Tsopano, ngati inu mwadzazidwa ndi dziko. . .Ndipo pamene inu muti mupulumutsidwe, inu mukhoza kukhala mutadzazidwa ndi malingaliro abwino, ndi zina zotero; koma kupatula ngati inu mwadzazidwa ndi Mulungu! Mulungu anatumiza Mzimu Woyera, ku dziko lapansi, kuti uzikauchititsa Mpingo.

<sup>63</sup> Ndipo inu mukhoza kudzazidwa ndi malingaliro. Inu mukhoza kudzazidwa ndi zamulungu. Ndipo inu mukhoza kudzazidwa ndi maphunziro, wodziwa zonse. Ndipo inu mukhoza kudzazidwa ndi chipembedzo, ndipo apobe nkukhala chandamale cha Mdierekezi. Ndiko kulondola. Tsopano, pamene. . .

<sup>64</sup> Mulungu anakupangani inu kuti muzikhoza kukhuthulamo. Pakuti, pamene inu munkabadwa, inu munapangidwa ndi malo oti muzidzadzitsidwa. Mwa chibadwa, ndinu mwana wa Mdierekezi. Ndipo pamene inu. . . Mlaliki akabwera kumeneko, ndipo inu mumalapa ndipo mumatsukidwa.

<sup>65</sup> Inu mukuona chiani? Mdierekezi amadza. Iye amabweretsanso kwa inu, ndi kudzakuikani inu mu chipembedzo china chaching'ono, ndi kuti, "Mpingo wathu ndi umene uli wawukulu." Inu mukulakwitsa, apo pomwe, pakuyamba nazo. Ndiye inu mumakhala ammutu, amalingaliro-apamwamba. "Chifukwa, izo sizimanditsutsa ine kukhala kunyumba ndi kumawonera televizioni. Izo sizimanditsutsa ine kuti ndizisuta ndudu yaing'ono pocheza kapena kutenga chakumwa, kamodzi mu nthawi." Zipatso zako zimanena chomwe iwe uli.

<sup>66</sup> Ndiyeno inu mudzamumva mlaliki wina akuimirira. Ndipo inu mukhoza kukhala kuti mumawerenga Baibulo, ndipo inu nkuwona pamene Yesu anapanga ndipo anachita zozizwitsa. Inu mkuzitengera izo kwa abusa. "O," iye akati, "tsopano, taonani. Ife sitimakhulupirira Izo." Ndi ndani "ifeyo?" Ndi ndani "ife samakhulupirira Izoyo"; iyeyo ndi ndani? Si iyeyo ndi Mulungu, pakuti Mulungu anawalemba Iwo. Ndi iyeyo ndi winawakenso.

<sup>67</sup> Ndipo ngati inu mungapite kuseri kwa izo, ndi cholinga chomwecho chomwe chinali pa nsanja ya Babulo, kuti adzimangire ufumu wopangidwa ndi munthu, wa mdziko lapansi. Koma Mulungu sakufuna izo. Iye samafuna nonse inu mukhale amodzi pansi pa Chimethodisti, pansi pa Baptisti, kapena pansi. . . zamipingo zirizonse, mutu wa mpingo. Iye sakufuna kuti inu nonse muyanjane pansi pa Roma. Iye sakufuna kuti inu nonse muyanjane pansi pa. . . ulamuliro wa mpingo uliwonse.

<sup>68</sup> Iye akufuna inu muyanjane pansi pa Ufumu Wake wauzimu, Mzimu Woyera. Ndipo pamene Mzimu Woyera udza, dziko limakhala lakufa, ndipo inu mumadzazidwa ndi ubatizo wa Mzimu Woyera. Ndipo Mdierekezi ndi munthu yemwe amayenera kukhala kutali ndi inu. Inu muli pansi pa ulamuliro wa Mulungu. Inu ndinu cholengedwa chatsopano. Mzimu Woyera umabwera mu malo opanda kanthu awo ndi kuwadzaza iwo.

<sup>69</sup> Tsopano, m'busa, kagulu kalikonse, zolemba zina zazing'ono zomwe inu mukanaziwerenga, zikhoza kunena kwa inu,

“Masiku a zozizwitsa anatha.” Awo ndi malo abwino kuti Mdierekezi azembetserepo umodzi wa mizimu iyo mmenemo ndi kukupangani inu kukhala munthu woyipisitsa yemwe inu mukanakhala pamene inu munali wochimwa. Chifukwa, wochimwa wachipembedzo ndiye woyipisitsa wa onse. Ndiye woyipisitsa. Yesu ananena chomwecho. Ndi mzimu woyipisitsa

<sup>70</sup> Ndiye inu mukhoza kupita ku msonkhano kumene kuli mphamvu yaikulu ya Ambuye! Ndipo chinthu choyamba chimene inu munganene, pamene inu munawona izo, “Tsopano, ine ndikungodabwa. Ngati ine ndisokonezedwa ndi Izi, iwo akandipatsa ine kalata yanga ku tchalitchi.” Mukuona pamene inu muli?

<sup>71</sup> Tsopano, mwinamwake sizitero. Uko kuli zipembedzo zabwino, azibusa abwino, Amethodisti, Abaptisti, mitundu yonse yosiyana omwe amakhulupirira mu kusuntha kwauzimu kwa Mulungu, omwe amakhulupirira kuti munthu amayenera kuti abadwe kachiwiri ndi kudzazidwa ndi Mzimu Woyera. Ndipo ine ndikuthokoza Mulungu chifukwa cha wina aliyense wa iwu. Alipo ambiri a iwo omwe amakhulupirira. Mulungu ali nawo ana Ake amamatira mu malo aliwonsewo. Koma chimene ine ndikuyesera kuti ndinene, mu unyinji inu mumapezamo izo, mipingo yonse iyo.

<sup>72</sup> Ine ndikufuna kuti ndikufunsemi inu anthu Achimethodisti chinachake, omwe simumakhulupirira mu machiritso Auzimu. Nanga bwanji Joni Wesile, woyambitsa wanu? Pamene iye ankakwera kavalo, kuti akamupempherere mkazi wodwala, ndipo kavaloyo anapunthwa mu dzenje la njale, ndipo anagwa ndipo anathyola mwendo wake. Joni anatsika pa kavalo wake, anatenga botolo la mafuta, ndipo anati, “Ambuye, Inu munamupanga kavalo uyu, chimodzimidzi momwe Inu munandipangira ine,” ndipo anamudzoza kavaloyo ndi mafuta. Ndipo anakwera pa iye ndi kumapita. Nanga bwanji izo? Inu mutalalikirira izo mu mpingo wa Methodisti wamakono lero, iwo angakuponyere iwe panja pakhomo. Ndithudi.

<sup>73</sup> Koma inu mukuona chomwe izo ziri? “Mayi wakale wachiwerewere,” wa mu Baibulo, Chivumbulutso 17, iye anali nao ana aakazi. Ndipo ndithudi ine sindikusowa kuti ndipite mwatsatanetsatane pa izo. Chiprotestanti ndi chobalidwa ndi Chikatolika. Ndithudi, izo ziri. Iwo anatulutsamo zinthu zawo zambiri, akukamirirabe kwa izo. Akumachitabe izo, kutali kwambiri ndi Kuphunzitsa kwa Mwamalemba, kutali kwambiri ndi Kuphunzitsa kwa atumwi.

<sup>74</sup> Iwo adzipangira okha Kachikhulupiriro ka Atumwi. Ine ndikufuna munthu wina aliyense kuti andiuze ine pamene atumwi ankabwereza konse—kachikhulupiriro monga choncho. Palibe, palibe! Koma inu mumatsamira kwa izo.

75 Ndipo inu mumawatchula ansembe anu, “Bambo.” Ndipo Yesu anati, “Musamutchule munthu aliyense ‘Bambo.’”

76 Ndipo inu anthu, inu mumatulutsa timabuku tanu tating’ono ta pemphero, onse Achiprotestanti ndi Akatolika, ndi kumanena mapemphero, mobwereza bwereza ndi kubwereza, onse Achiprotestanti ndi Akatolika. Ndipo Yesu anati, “Musamabwerezebwereze mwachabe monga akunjya amachitira; kuganiza kuti akhoza kumvedwa, pakuyankhula kwawo kochulukika.”

77 Inu mukuona, m’phika sungakhoze kunena ketulo kuda. Ndi kulondola. Zonsezo ziri pansi pa chiweruzo, maganizo aliwonse opangidwa ndi munthu. Ndipo ndicho chifukwa mu chitsitsimitso chonga ichi, chikabwera ku mzinda, mipando iyi ili yosakhalidwa. Koma Mulungu awutumiza Iwo, mulimonse, ndipo mapepala alengeza Iwo. Ndipo pa Tsiku la Chiweruzo, pamene inu mudzaitanidwa kuti mukayankhe, inu mudzapezeka wolakwa monga iwo anali kumbuyo uko.

78 Kodi Yesu sanati, “Mfumukazi yaku Sheba, Mfumukazi ya Kummwera, inabwera njira yonse kuchokera ku madera akutali a dziko,” atakhala pa nsana wa ngamila, miyezi itatu, “kuti adzawone mphatso ya Mulungu, yemwe anali Solomoni”? Iye anati, “Indetu, ine ndikuti kwa inu, wamkulu kuposa Solomoni ali pano.”

79 Ndipo ine ndikuti, usikuuno, kuti wamkulu kuposa Solomoni ali pano. Ndi Umunthu wa Khristu, mwa Mzimu Woyera, akuchitachita ndi kugwira ntchito, kumazichita mu moyo wa munthu monga Iye ankachitira kuno.

80 Mulungu anakupangirani inu malo omwe angakhale opandamo kanthu. Tsopano, inu simungangoti mungowupukuta moyo wakalewo. Inu simungakhoze kuwupatsa moyo wakale kukonza kwa nkhope. Iye ayenera kuti afe, ndipo moyo watsopano ukhale utabadwa mwa iye. Iye samasowa zozipakapaka zina kapena ndi chiyani chimene inu mumaika pa milomo panu, zomwe akazi amachita, inu mukudziwa, zowapangitsa iwo kuti aziwoneka bwinoko. Iye samasowa kupotolapotola tsitsi lake. Iye samasowa zinthu za pa milomo. Mpingo ukusowa Kubadwa ndi kudzazidwa ndi Mzimu Woyera.

81 Ndi tsitsi lake atalipotapota ndi milomo yake atailocha, iye akadali msungwana wakale yemwe uja. Iye akadali wokaikira. Iye akadali, ali ndi zokaikira zake. Iye akadali ndi mantha ake. Iye wangodzisokoneza yekha. Ndipo iye sakufuna kuti achimve Choonadi, chifukwa chinthu chomwe chiri mkati mwa iye sichingamuloleze iye kwa izo. Ndiko kulondola. Ndithudi.

82 Mkazi wa mbiri-yoyipa pa misewu, iwe ukayenda ndi kukamuza iye, “Hei, mkazi, iwe ukulakwitsa.”

Iye ati, “Samala ntchito yako yako.”

83 Ndipo membala wina wowuma khosi ndi woyipa kaseveni kuposa mkazi ameneyo.

84 Kumuuza iye, “Kuli chitsitsimutso chachikulu chiri kuchitika. Inu muyenera mubwere kumeneko. Ambuye Yesu adziwonetsera Iwowokha, pakuchiritsa odwala. Anthu ali, zina zotero, akulandira Mzimu Woyera.”

85 “Pitirirani nazo! Kodi chikukuvuta ndi chiani? Ine ndiri pa mpingo. Ndine wabwino monga iwe.” Chifukwa? Iye sakudziwa bwino mulimonse.

86 Koma inu mukayankhula kwa mkazi wakhalidwe labwino ndi kumuuza iye kuti ndi kulakwitsa kuchita izo. Iye angati, “Ameni. Ine ndikudziwa uko ndi kulakwitsa.”

87 Ndipo inu mukamuuza mwamuna kapena mkazi, yemwe ali wobadwa kachiwiri mwa Mzimu wa Mulungu, kuti ubatizo wa Mzimu Woyera uli pano kwa iwo, kuti udzazitse mtima wawo. Iwo angafuule “ameni” kwa Izo, pakuti iwo amadya ndi kukhalamoyo pa Mawu a Mulungu. Ndithudi, iwo amatero.

88 Koma, inu mukuona, monga izo ziriri mu dziko chomwecho izo ziri mu mpingo. Iwo akuyesera kuti amange chinachake. Mulungu sakusowa thandizo lanu kuti amange Ufumu Wake. Mulungu akungofuna kuti inu muzilalikira Mawu. Iye azichita zomangazo. Iye ndi wazomangamanga. Iye ali nawo mapulani ayalidwa Apa kuno. Chabwino.

89 Kodi ife timachita chiani ndiye? Mulungu anakupangirani inu malo oti muzidzikhuthula, zinthu za mdziko. Tsopano, chibadwa chimawuyika mzimu mmenemo womwe umakupangitsani inu kumakonda zinthu za mdziko, ndipo inu mumadziwa kuti inu mukulakwa pamene inu muchita izo.

90 Kaya ndinu membala wa mpingo, inu mukhoza kukhala basi wachipembedzo monga momwe inu mungakhoze kukhalira, ndipo muli wodzaza basi ndi Mdierekezi, nacho. Ndiko kulondola. Ngati inu muwakaikira Mawu a Mulungu, Mawu aliwonse a Iwo kuti ali owona, ndi Mdierekezi akukuuzani inu izo. Ndithudi, iye ali. Uwo ndi mwano. Koma ndi nthawi, nthawi yakwana kuti mlaliki wina wochita mwachikazi avule magolovesi ake ndi kumalalikira Uthenga momwe Iwo unalembedwera, ndi kusiya kumasewera apa ndi zomuchitikira zina za ku seminare.

91 Ine nthawizonse ndimamva chisoni ndi nkhuu ya muhofungatira. Nkhuu yomwe inabadwira mu chofungatira, imalira, ndipo ilibe manthu woti azipitako. Izo zikundiyyikira mu malingaliro za mlaliki waku seminare yemwe samadziwa mochuluka za Mawu a Mulungu kuposa zomwe seminare inanena; kumalira, ali wopanda Mayi woti azipitako.

92 Koma pamene iwe wabadwa kwenikweni pansu pa mapiko a chisomo Chake ndi mphamvu, iwe umagwirizana ndi Mawu

aliwonse amene Iye ananena, kuti ali Choonadi. Ndipo pamene Mulungu asuntha mu zauzimu, mtima wanu umachitira njala kwa Iwo.

<sup>93</sup> Inu simumapita pambali ndi kukati, “Kuwerenga maganizo! Mdierekezi! Belezebule! Ine sindikuzikhulupirira Izo. Mpingo wanga sumaphunzitsa Izo!”

<sup>94</sup> Inu mumati, “Mulungu atamandidwe kwanthawizonse,” pakuti inu mwadzazidwa. Inu simungangokhala opanda kanthu.

<sup>95</sup> Kupanda kanthu ndi kusakhala ndi chochita. Ndilo liri vuto ndi otembenuzidwa lero. Mwamsanga pamene inu mutembenuzidwa, inu mumayamba kusakhala ndi chochita. Inu muyenera kumakhala muli uko pa mawondo anu, mukufunafuna Mulungu pofuna Ubatizo wa Mzimu Woyera, kuti mudzazidwe nao. Ndiye inu muli nalo khoma, Kukhalapo Kwake kodala limodzi nanu. Ndipo pamene mdani abweramo, ngati mkango mu khola usiku uja ndi Daniele, Kuwala kwa Mulungu kumawalira apo ndipo iye amachoka kwa inu, “Ngati mwamuna wabwino wa mnyumbamo sanaitchingire iyo.” Ndithudi.

Tsopano, mchijanano, pa Tsiku la Pentekoste.

<sup>96</sup> Kapena, basi izo zisanachitike kumene, ophunzira onse anali atatsukidwa kwathunthu, machimo awo onse anali atakhululukidwa. Ndipo Yesu, M’busa, nkhuu yaikulu, monga izo zinali, monga Iye anati Iye “akanati awasonkhanitse iwo monga nkhuu,” anapiye Ake. Ndiye, pamene mzimu wa Mdierekezi unachotsedwamo, kuyembekezera nthawi yodzazidwa.

<sup>97</sup> Ndipo, apobe, mu zonse izo, amuna thwelofu okha, mmodzi wa iwo anapeza kudzoza kwa Mdierekezi, ndipo iye atamuwona kale Yesu akuchita ntchito zabwino zonse izo. Iye anali mmodzi yemweyo amene anawatsogolera asilikari kuti ayike chiguduli kuzungulira mutu Wake, ndi kumamumenya Iye pa mutu ndi chibonga kapena ndodo, ndi kumati, “Tiuze ife ndani wakumenya Iwe. Ife tikukhulupirira Iwe.” Atamutsatira kale Yesu ndipo atawona zozizwitsa Zake, ndi kumva. Myuda anadza, ndipo Yesu anamuza iye yemwe iye anali, kumene iye anali kuchokera. Atawona kale zonse izo, munthu yemweyo anazikaikira izo, atamuwona kale Iye pa chitsime ku Samaria, ali ndi mkazi, atamuza iye machimo ake. Ndi kumumva Mfarisi akuti, “Iye ndi wambwebwe.” Ndiyeno atamuwona kale Yesu wokondedwa, mkazi atakhudza chovala Chake ndi kuchiritsidwa, iye sanali kukhulupirira apobe. Ndipo analoleza mzimu wa kusakhulupirira kuti ubwere mwa iye, chifukwa iye anali atalanzidwa mwakunjako. Mukuwona zomwe ine ndikutanthauza?

<sup>98</sup> O, ndi chinthu choyipa bwanji kusakhulupirira kuli! Ndipo komabe, anthu amadzinenera Chikristu, nkumakhala

ndi icho mwa iwo. “Ammutu, amalingaliro-apamwamba,” Baibulo linati, “mu tsiku lotsiriza.” Kodi ine ndikumverera mwachilendo ndi izo? Ayi, bwana. Izo zikundipangitsa ine kudziwa izi, kuti nthawi yotsiriza ili pafupi. Pakuti Baibulo linati, “Mzimu ukuyankhula mwachimvekere,” inu mukudziwa chomwe mawu okuti *mwachimvekere* akutanthauza, “kuti mu masiku otsiriza,” ndiwo anowa, “nthawi zowopsya zidzaza, pakuti anthu adzakhala ali odzikonda okha.”

<sup>99</sup> “Ndine Dr. Ph.D. Jones, ndi c—chondichitikira changa cha ku seminare. I—ine ndiri nao madigirii anga onse. Ndine LL, ma L awiri, D. Abusa athu ali ndi zonse *izi, izo.*” Izo ziribe kanthu kamodzi kochita ndi Mulungu

<sup>100</sup> Ine ndinali ndi munthu anabwera, osati kale litali, anati, “M’bale Branham, ine ndikhoza kumata khoma lanu ndi madigirii.” Ndipo anati, “Nthawi iliyonse, pamene ine ndimapeza digirii yanga ya udokotala, ine ndinkaganiza kuti ine ndinamupeza Khristu. Pamene ine ndinapeza digirii yanga ya zolemba, pamene ine ndinapeza digirii yanga ya ubachala, ine ndinamusaka Khristu mu zonse izo. Ndipo ine sindinamupeze Iye panobe.” Iye anati, “Kodi aphunzitsi akhala akulakwitsa?”

<sup>101</sup> Ine ndinati, “Khristu samadziwidwa ndi madigirii a zamulungu izi, koma Iye amadziwika mu umunthu wa Mzimu Woyera umene unadza pa Tsiku la Pentekoste.”

<sup>102</sup> Ndipo munthuyo anagwera pa tebulo langa la khofi, mu chipinda changa chodyera, ndipo apo analandira Mzimu Woyera. Amen. Ali ku ntchitoyi usikuuno, akulalikira machiritso Auzimu, yemwe ali mmodzi wa amuna odziwika a tsikuli. Kodi mpingo unachita chiani? Unamuchotsa iye, mwamsanga ndithu. “Odala muli inu pamene iwo adzakuchotsani inu mu masunagoge ndi zinthu, chifukwa cha Dzina langa.”

<sup>103</sup> Chimene Baibulo linati, “Iwo adzakhala ammutu, amalingaliro-apamwamba.” Liti? “Mu masiku otsiriza. Okonda televizioni, zosangalatsa, kuposa kukonda Mulungu. Ophwanya chipangano, otsutsa mwabodza.”

<sup>104</sup> “Tsopano ine ndikukuuzani inu. Musati mupite uko ku msonkhano umenewo, chifukwa kulibe kanthu kwa izo.” Otsutsa mwabodza! Baibulo linanena chomwecho. “Okhala nawo mawonekedwe aumulungu, koma kumakana mphamvu yakeyo.” Ndi mphamvu yanji iyo?

<sup>105</sup> Ophunzira anafunsa. Mphindi yokha. Ophunzira anafunsa funso ili pamene iwo anawona kuti Yudasi anali atamupereka Iye ndipo chirichonse chinali pafupi. Iwo anati, “Ambuye, kodi Inu pa nthawi yino mubwezeretsa ufumu kwa Israeli?” Penyani zomwe Iye ananena. “Izo siziri kwa inu kuti mudziwe ora limenelo. Koma pitani uko ku mzinda wa Yerusalemu, ndipo inu mukadzazidwa ndi mphamvu yochokera Kumwamba inu musanakhale mboni.” Mboni iyenera kuti izidziwa chinachake.



Mboni iyenera kumakhala ndi chomuchitikira. Ndipo inu simungakhoze kukhala mboni za Khristu mpaka Mzimu Woyera utakubatizani inu.

<sup>106</sup> Yesu sakadawalola ophunzira Ake kuti azikalalikira Uthenga mpaka iwo atalandira Mzimu Woyera. Komabe, iwo anali atapatsidwa ulemu woti aziyenda ndi Iye, zaka zitatu ndi theka. Ngakhale iwo anali anthu oyera, olandiridwa pamaso Pake, koma Iye sakadawalola iwo kuti apite kumakalalikira mpaka iwo atayembekezera kumeneko atachotsa kusiyana konse mwa iwo, ndiyeno Mzimu Woyera unadza.

<sup>107</sup> Chimene dziko likusowa lero ndi kudzazitsa komweko. Pamene kukhuthula kwabwera, ilo likusowa kudzazidwa. Kodi kudzazitsa uko kumachita chiani pamene Iko kubwera umo? Kumene inu muli ndi kukaikira, iko kumabweretsa chikhulupiriro. Kumene inu muli ndi kusiyana, iko kumabweretsa chikondi. Kumene inu munali ndi udani, iko kumabweretsa chiyanjano.

<sup>108</sup> Ndiyeno, pamene, Mpingo wa Mulungu wamoyo tsiku lina udzagwirizana pansi pa Mutu umodzi waukulu, ndipo uwo udzakhala uli m—Mutu wa Mulungu. Mulungu, ndipo mu chiyanjano cha Thupi la Khristu, adzakhala ali Kazembe ndi Mfumu ndi Ambuye, pa Mpingo wonsewo, pansi pa ulamuliro Wake. Ndiye iye adzaldiridwa mmwamba.

<sup>109</sup> Lero, masanja onse a Babulo iwo akhoza kuwamanga, maroketi onse omwe iwo angawapeze, chisosholismu ndi chikomunisi zomwe iwo akhoza kuzitakasa, machitidwe onse azampingo zidzalephera. Koma mosasamala izo zonse, Mulungu adzakhala nawo Mpingo wogwirizana pansi pa Mfumu Yake, pansi pa Ufumu Wake, mwa ubatizo wa Mzimu Woyera.

<sup>110</sup> Yesu anati, “Zizindikiro izi zidzawatsata iwo amene akhulupirira: mu Dzina Langa iwo azidzatulutsa ziwanda; azidzayankhula ndi malirime atsopano. Ngati iwo anyamula njoka kapena kumwa kanthu kakupha kalikonse, iko sikamadzawapweteka iwo. Iwo azidzaika manja pa odwala, iwo azidzachira.” Zizindikiro zazikulu ndi zodabwitsa! “Ntchito zimene Ine ndikuchita inunso muzidzazichita. Ngakhale zochuluka kuposa izi iwo azidzazichita, pakuti ine ndikupita kwa Atate. Kanthawi pang’ono dziko silindiwonanso Ine, komabe inu muzindiwona Ine, pakuti Ine ndikhala ndiri nanu.” Chiani? Kukhuthula, kutsanula. “Ndiye Ine ndidzakhala ndiri mwa inu, mpaka kumapeto a dziko, chitsirizitso.” Ndithudi. “Ine ndidzakhala ndiri nanu, ngakhale mkati mwanu, mpaka kumapeto a dziko.”

<sup>111</sup> Pamene Mzimu uwo uli mmenemo, Iwo umagwira Mawu Amuyaya a Mulungu, ndipo Iwo umachitcha chirichonse chotsutsana ndi Iwo ngati kuti icho palibe, ziribe kanthu chomwe chichitika, chimene dziko likunena, chimene china

chirichonse chikunena. Ngati Mulungu wapanga lonjezo, munthu yemwe wadzazidwa ndi Mzimu umenewo agwiritsabe kwa lonjezo ilo la Mulungu, chifukwa palibe china chirichonse mu njira yake.

<sup>112</sup> Mpingo uli wangwiro. Mpingo uli wotsukidwa ndi Mzimu Woyera. Chikumbumtima chawo, mantha a kukaikira ndi kusakhulupirira zachotsedwamo. Ndipo pamene iwo amva Mawu a Mulungu akunena chinthu chinachake, iwo amawakhulupirira Iwo. O! Iwo amagwiritsabe kwa Iwo. Iwo samasuntha basi kwa Iwo.

<sup>113</sup> Ndipo dziko lero, mzanga, likufuna kuti liwaone anthu omwe alumikizana ndi Khristu, kuti aziwonetsera Mzimu weniweni woona wa Khristu. Ngwazi zolimba!

<sup>114</sup> Potseka, ine ndikhoza kunena kuti, dziko likufuna kuti liwone ngwazi. Iwo amazilemekeza ngwazi. Izo nzabwino. Mwambi wakale uli, woti, “Amantha amafa nthawi kamilioni, pamene ngwazi sizimafa konse.”

<sup>115</sup> Pali nthano imene ikubwera ku malingaliro anga. Ine ndikanafuna kuti ndiyibwereze iyo kwa inu kwa mphindi pang’ono zokha. Iyo ndi nthano ya ngwazi yomwe kambirimbiri imaiwalidwa. Ambiri a amuna inu, ausinkhu wanga, ndi inu akazi, inu mukuikumbukira iyo bwino mu mabuku athu aku sukulu.

<sup>116</sup> Zinali zaka zambiri zapitazo, mu Switzerland. Anthu aang’ono achi Swiss anali atapita mu mapiri umo ndipo anakadzimangira okha nyumba zina. Iwo anali nacho chuma chawo chawo chochepa, ndi zina zotero, manyumba awo aang’ono. Ndipo iwo ankawakonda iwo. Iwo sanali anthu ankhondo. Iwo anali anthu amtendere.

<sup>117</sup> Ndipo zonse mwakamodzi, nthawi yina, akubwera mu Switzerland, anali gulu lalikulu lamphamvu la nkhondo. Ndipo iwo anali amuna ophunzitsidwa bwino, atangokhala apo monga mipando iyo apo, basi monga khoma la njerwa; zishango zazikulu, nthungo zazikulu, amuna ankhondo ophunzitsidwa bwino. Ndipo iwo anabwera akuguba kulowa mu Switzerland, kudzatenga zomwe achi Swiss anali nazo.

<sup>118</sup> Ndipo achi Swiss, pofuna kuti atetezere manyumba awo, kuwapsyopsyona akazi awo tsalani bwino, ndi ana awo ndi makanda, iwo anatenga zidutswa zazing’ono za zotchetchera, matanthwe ndi miyala, zibonga zazikulu zakale, ndipo anapita uko mu chigwa, kuti akakomane ndi ankhondo okudza. Ndipo pamene iwo anakasonkhana uko, amuna apang’ono okha ongokwanira mdzanja, ndipoponse powazungulira iwo panali ankhondo aakulu akuguba. Kodi iwo akanachita chiani? Iwo anaima opanda chiyembekezo, opanda wowathandiza, wina akuyang’ana pa mzake. Iwo anali atagonjetsedwa. Panalibe njira yozungulira nayo apo. Iwo anali atathedwa.

119 Patapita kanthawi, kunali mwamuna dzina lake Arnold von Winkelried. Iye anatulukira, ndipo iye anati, “Amuna aku Switzerland, kungwoloka phiri kuli nyumba yaing’ono yoyera kumene mkazanga ndi ana aang’ono atatu akuyembekezera.” Anati, “Pamene ine ndinawapsyopsyona iwo tsalani bwino, mmawa uno, ine sindidzawawonanso iwo kachiwiri pa dziko lapansi lino.”

120 Iwo anati, “Arnold von Winkelried, kodi iwe uchita chiani?”

Iye anati, “Tsiku lino, ine ndifera Switzerland.”

121 “Chabwino,” iwo anati, “Arnold von Winkelried, izo sizichitira ubwino uliwonse. Nchifukwa chiani iwe ukuti ufera Switzerland?”

122 Iye anati, “Inu mutenge zomwe muli nazo; chometera ubweya, zikwakwa zakale zazing’ono, ndodo ndi zibonga, miyala.” Anati, “Inu munditsatire ine, ndipo inu mukamenye mopambana momwe inu mungakhazere ndi zomwe inu muli nazo.”

Anati, “Kodi iwe uchita chiani?”

123 Ndipo iye anaponyera pansu chikwakwa chake, chinthu amati akamenyere nacho. Iye anakweza mmwamba manja ake, ndipo iye anafuulira kwa ankhondo aakulu awo.

124 Iye anayang’ana pozungulira. Iye anawona pomwe panali nthungo zothinanitsa. Basi aliyense ali mu chiwerengero chofanana, akuwagubisa iwo kutsatira phiri, kupitirira, pitirira. (O, ndi momwe Mdierekezi amachitira izo.) Kuwagubisila iwo ku ngodya.

125 Iye anakweza dzanja lake, ndipo iye anafuula, “Pangani njira ya ufulu!” Ndipo ankhondo obwerawo anadabwa nchiani. Ndipo iye anayamba kuthamanga, ndipo iye anafuula kachiwiri, “Pangani njira ya ufulu!”

126 Ndipo pamene iye anafika kumene mu gulu lalikulu ili la nthungo, kumene ambiri analoza, kuti amugwire iye, iye anagwira mikono yake monga *chonchi*, ndipo anatenga nkono wonse wodzaza ndi nthungo izo ndipo anazitengera izo mchifuwa mwake. Kuwonetsera koteroko kwa ungwazi weniweni, izo zinawasokoneza ankhondo aakulu awo, ndipo izo zinawagwiritsa iwo.

127 Apa panadza achi Swiss, ali ndi zibonga ndi ndodo, ndipo anawamenya ankhondo awo kuwatulutsa mu fuko lawo. Ndipo iwo sanayambe akhalapo ndi nkhondo kuyambira pa nthawi iyo mpaka pano, chifukwa munthu mmodzi anachita gawo la ungwazi ndipo anachita zomwe zinali zolondola. Izo sizinayambe zapedwapo, ndipo kawirikawiri sizimafanizidwa, ngati ungwazi.

128 Koma, o, ndicho chinthu chaching’ono chotero, kwa tsiku limodzi, zaka zambiri zapitazo, pamene ana a Adamu, mtundu

wa dziko lino, unapanikizidwira ku ngodya, ndi kudwala ndi matenda ndi tchimo. Iwo anali atatuzidwira aneneri, ndipo anawapha iwo. Ndipo iwo, mitundu yonse ya malamulo, ndipo anazikana izo. Mtundu wa Adamu unapanikizidwira ku ngodya.

<sup>129</sup> Analipo Mmodzi Yemwe anatsika kuchokera Kumwamba, ndipo anati, “Ine ndikupita uko ku dziko lapansi lero kuti ndikapereke moyo Wanga.” Iye anapeza pamene panali patawiriritsa mivi. Ndipo mantha a kwa mtundu wa Adamu anali imfa. Iye anaigwirra imfa, pamene Iye anali kupita ku Kalvare, ndipo anaikokera iyo mu chifuwa Chake.

<sup>130</sup> Ndipo Iye anawauza ophunzira Ake, “Khuthulani tsopano. Pitani kutali... Mukayembekezere kutali uko mpaka Ine nditakutumiziranso inu Chinachake choti muzimenyera nacho.” Lidalitsike... Mundikhulukire ine. Likhale lodalitsika Dzina la Ambuye. Iye anatomiza Mzimu Woyera, ndipo anati, “Zinditsatirani Ine. Anadulira tchimo ndi matenda ku khoma.”

<sup>131</sup> Amuna ndi akazi, chinthu chachikulu chimene chinayamba chaperekedwa kwa Mpingo wa Mulungu si kugwira zikalata zina zamipingo mdzanja lako, koma kuti udzazidwe ndi Mzimu Woyera wa Mulungu, ndi kuwudula ufumu wa Mdierekezi mpaka Mtsogoleri wathu Wamkulu atadza kudzatenga ulamuliro.

<sup>132</sup> Mulungu akudalitseni inu. Musaganize kuti ine ndasokonezeka. Izo ndi zoon. Ine ndikudziwa zomwe ine ndikuzikamba. Amuna aulemu; akazi, inu omwe mukukhulupirira mwa Mulungu; inu omwe mukudzinenera kuti muli nawo Mzimu wa Mulungu mu mtima wanu. Ngati inu mukudwala kapena mukusowa, inu muli nacho chida apo kuti mumenyere nacho matenda awo. Icho chiri mwa inu. Mulungu anachipereka icho kwa inu.

<sup>133</sup> Bwanji kuti ife tiziyima mmbuyo ngati amantha? Bwanji kuti tiziima chapambali? Tiyeni tizimutsatira Mtsogoleri. Tiyeni timutsatire Iye Yemwe anapita ku Kalvari. Pamene Iye anapita ku Kalvari, “Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu. Ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa.”

<sup>134</sup> Tengani izo zomwe Iye wakupatsani inu, ndipo muzimenyana ndi matenda ndi tchimo. Muzimenyana ndi kusakhulupirira kuchoke. Muzimuza Mdierekezi kuti iye ndi wabodza. Khristu anati Iye waligonjetsa dziko. “Wamkulu ndi Iye yemwe ali mwa inu kuposa iye yemwe ali mdziko.” Yaikulu ndi mphamvu ya Khristu, mwa inu, kuposa matenda awo omwe inu muli nawo mu thupi mwanu usikuuno. Yaikulu ndi mphamvu ya Khristu, kuposa katchimo kakang’ono ako, kofooketsa kamene inu simukukhoza kukagonjetsa. Tiyeni tiutenge Mzimu Woyera uwo ndipo timumenyere nawo Mdierekezi, ndipo tiziyenda mwachigonjetso, ngati ngwazi za mtanda.

Tiyeni tipemphere.

135 Yehova, Yehova-rafa, Yehova-yire, ife tikudza mu Dzina la Yesu. Ife tikudza chifukwa Iye anati, “Apempheni Atate chirichonse mu Dzina Langa, Ine ndidzachichita icho.”

136 Pano pali gulu laling’ono la anthu apa, usikuuno, omwe akuzandima panjirayi, kuyesera kuti akhale pansu pa mbendela, ndipo Mdierekezi akuchitira ukali pa iwo. Iwo akuyang’ana kunja uko pa khoma lalikululo ilo la ankhondo omwe awazungulira iwo, ndipo akuwauza iwo, “Masiku azozizwitsa anapita, ndipo palibe chinthu choterocho.”

137 O Ambuye Mulungu, muwalole iwo agwiritse kugwira uko kwa Moyo Wamuyaya uwo umene wadzazitsa mtima wawo, Mzimu Woyera. Ndipo ngati Iye sanawadzaze iwo; mulole Iye achite izo pakali pano. Mulole kukaikira konse kuchokemo. Ndipo mulole thupi laling’ono ili la anthu, usikuuno, lidzazidwe ndi mphamvu yodzazitsa ya Mulungu, kuti itenge malo a kusakhulupirira ndi kukaikira. Ndipo muwapatse iwo chikhulupiriro, ndi chikondi, ndi chisangalalo, ndi chimwemwe, ndi Mzimu Woyera, kuti agwiritse lonjezo ilo limene Mulungu analipereka, monga Abrahamu wakale, ndi kumatcha zinthu, zomwe palibepo, ngati kuti zilipo, chifukwa Mulungu ananena chomwecho. Perekani izo, Ambuye.

138 Pomwe ife tiri ndi mitu yathu yoweramitsidwa,ponseponse mu chipinda chino, ine ndikudabwa ngati mungakhale munthu muno wopanda Mzimu Woyera, usikuuno, anganene, “O Ambuye, ndichitireni chifundo ine. Ine ndikuchita manyazi kuti ndikupezeka ndiri cha ku nsanja izi za kachitidwe kazamipingo kopangidwa ndi anthu, ka kukaikira konse uku ndi zinthu zomwe iwo akubala nazo. Ambuye, ndichotsenimo ine mu ufumu uwu, usikuuno, ndipo ndiyikeni ine mu ufumu Wanu, mwa ubatizo wa Mzimu Woyera. Ine ndikuwufuna Iwo tsopano, Ambuye. Ndipatseni ine chikhulupiriro kuti ndizikhulupirira machiritso anga. Ndipatseni ine chikhulupiriro kuti ndizikhulupirira kuti machimo anga achoka, ndi zinthu zonse izi. Ndipatseni ine chikhulupiriro chotero kuti Mzimu Woyera ubwere mwa ine ndipo ungozifukiritsa moyo wanga ndi chisangalalo.” Kodi mungakweze manja anu kwa Iye ndi kuti, “Ine ndikufuna kuti ndiulandire Iwo?”

139 Mulungu akudalitseni inu, dona. Mulungu akudalitseni inu, inu, inu, inu. Ponseponse mchipindamu. Mulungu akudalitseni inu kumbuyo uko, dona. Ine ndikuyembekezera. Mulungu akupenyenera. Ndi inu cha apa, mzere wonse uwu muno. Inde. Mulungu akudalitseni inu.

140 “Ine ndikufuna Mzimu Woyera. Ine ndatopa, kumayendayenda, moyo watheka. Kupsyantima, ndi makangano ndi kulundirana, ndi kukaikira ndi mantha zonsezo ziri mu mtima mwanga, M’bale Branham, koma ine ndikuzifuna zonse izo zitulukemo. Ine ndikufuna kuti ndikhale pamalo

pomwe ine ndingakhale kuwala kowala. Ine ndikufuna ine ndikhale, moyo wanga, ukhale wonga wa Stefano, momwe iye analiri wopanda mantha.”

<sup>141</sup> Iwo anati nkhope yake inawala ngati mngelo. Iyo sikanati ikhale ndi kuwala konyezimira. Mngelo akanakhala wolimba. Iye akanamadziwa zomwe iye akuziyankhula. Iye anaima pamaso pa Bwalo lamilandu la Sanhedrin ndipo anati, “Inu owuma-khosi, osadulidwa, mu mtima ndi makutu! Inu mumaukaniza Mzimu Woyera. Monga momwe atate anu ankachitira, chomwecho inu mukuteronso.” Anali mngelo. Iye anali nao uthenga. Mawu oti *mngelo* amatanthauza “mtumiki.”

<sup>142</sup> “Ndipatseni ine, ndipangeni ine mtumiki, Ambuye, wa mphamvu Yaumulungu ya Khristu, mwa Mzimu Woyera mu mtima mwanga.” Kodi inu mungakweze dzanja lanu, winawake yemwe sanatero?

<sup>143</sup> Madalitso pa inu, bwana. Madalitso pa inu, dona wamng’ono. Mulungu akudalitse iwe, mnyamata. Ambuye akukuwona iwe. Zabwino. Chabwino.

<sup>144</sup> Tsopano ndi mitu yanu yoweramitsidwa, tiyeni tipemphere kuti Mulungu akudzazeni inu ndi Mzimu Woyera, apo pomwe pamene inu muli.

<sup>145</sup> “M’bale Branham, inu mukufuna kuti mubwere kuno, mudzayike manja anu pa ine, pofuna Mzimu Woyera?” Ine sindikusowa kuti nditero.

<sup>146</sup> “Pamene Petro ankayankhula Mawu awa ku nyumba ya Konerio, Mzimu Woyera unagwera pa iwo omwe anamva Mawuwo.” “Chikhulupiriro chimadza pa kumva,” osati kusanjika kwa manja, koma pakumva, “kumva (chiani?) Mawu a Mulungu.”

<sup>147</sup> Ine ndayesera, mwa njira yanga yodzichepetsa, kuti ndikusonyezeni inu nsanja zomwe ziri kumangidwa, nsanja za Babeloni zomwe ziyenera kuti zigwe. Ndipo ine ndikukulozerani inu ku Nsanja. Ndipo pali msewu umodzi wokha wopitira kwa Iyo, ndiyo mwa Mzimu Woyera.

<sup>148</sup> Inu simungakhoze kukhala pakati. Baibulo linati, mu tsiku lino, kuti, “Munthu aliyense yemwe sanali wosindikizidwa ndi Mzimu Woyera akanadzakhala nacho chilemba cha chirombo.” Kodi chilemba cha chirombo ndi chiani? Kusakhulupirira. Kodi inu simukudziwa chomwe iwo ali...ngati abusa anu akuphunzitsani inu. Mu Chipangano Chakale, pamene lipenga linkarira, ngati munthuyo akufuna kuti apite ali mfulu, iye amakhoza kupita ali mfulu. Ngati iye samafuna, iye amakhoza kuyenda kupita ku mtengo ndipo anali kumubowola khutu lake ndi chobowolera, chifukwa iye anakana kuti apite mfulu. Ndipo ngati iwe ukana kuti ukhale mfulu, ndiye iwe uzimutumikira bwana wa ntchito imeneyo tsiku lako lonse, ndipo iwe wataika.

149 “Kodi chisindikizo cha Mulungu ndi chiani, M’bale Branham?” Mzimu Woyera.

Inu mukuti, “Ndi Mwamalemba izo?” Mwamtheradi, ambiri a iwo.

150 Ndiroleni ine ndikupatseni inu amodzi kuti inu musaziiwale izo. Aefeso 4:30 amati, “Musawukwiyitse Mzimu Woyera wa Mulungu, umene inu munasindikizidwa nawo mpaka tsiku la chiwombolo chanu.” Ndi chimenecho Chisindikizo cha Mulungu. Ndizo zomwe ine ndikuyesera kuti ndikuuzeni inu. Inu mwachiyang’anira Chisindikizo cha Mulungu kuti chidze mu tsiku lotsirizali. Icho sichiri pa mphumi panu. Anati icho chiri pa *mphumi* panu ndiyo “nzeru, kuti muzimvetsa.” Koma Baibulo linati Chisindikizo cha Mulungu ndi ubatizo wa Mzimu Woyera. Ndipo aliyense yemwe ali nawo Iwo, mitima yawo ili yomasuka. Iwo ali osindikizidwa ndi nzeru ya Mulungu, mu mphumi zawo, kuti iwo akudziwa kuti Yesu anafa ndipo anauka kachiwiri, chifukwa iwo akukhoza kumamuwona Iye.

151 “Kanthawi pang’ono, ndipo wosakhulupirira sadzandiwonanso Ine. Komabe, inu muzindiwona Ine,” iwo omwe ali nacho Chisindikizo, “pakuti Ine ndikhala ndiri ndi inu, ngakhale mkati mwanu, mpaka kumalekezero a dziko. Ntchito zomwe Ine ndikuzichita inunso muzidzazichita, ngakhale zazikulu kuposa izi, pakuti ine ndikupita kwa Atate Anga.”

152 Dziko losakhulupirira likuyenda chopitirira mu mdima wokhudzika, chaku nsanja ina ya Babulo. Kukhudza, ndipo iwo ali ndi chinachake chimzake chapa zamatsenga zina, kagulu kena. Pamene, wokhulupirira weniweni ali ndi zizindikiro ndi zodabwitsa, ndipo izo nzobisika kwa maso a wosakhulupirira. Tsegulani mitima yanu tsopano ndipo mumulole Iye alowemo.

153 Ndati ndiwapemphe atumiki ena, apanso, mu nyumbayi, zipempherani makamaka pa nthawi ino.

154 Ino ndi nthawi yopambana. Nthawi iyi isindikiza kopita, mopanda kukaika, kwa ambiri. Moyo umodzi mtengo wa maiko teni sauzande! Ndi yopambana bwanji nthawi iyi.

155 Ambuye Mulungu, Mlengi wa miyambi ndi dziko lapansi, Yehova, fikirani pansu pakali pano mwa zifundo za Ambuye Yesu, Iye Wodalayo, ndipo tsanulirani Mafuta Opatulika a Mzimu Wanu mu mtima uliwonse pano, iwo amene ali a njala. Izo zinalembedwa mu Baibulo, “Pamene Petro anali chiyankhulire mawu awa, Mzimu Woyera unagwera pa iwo.” Palibe zodabwitsa; iwo onse anali aludzu. Inu munati, “Odala muli inu pamene inu muchita njala ndi ludzu pofuna chilungamo, pakuti inu mudzadzazidwa.”

156 Ife tingakhoze bwanji kuyankhula kwa anthu za Khristu pamene iwo alibe ludzu lofuna Iye? Pamene, iwo akumakhala mu maganizo awo opangidwa ndi anthu, ndi kukhutitsidwa,

osamadziwa kuti iwo ali “omvetsa chisoni, opandapake, akhungu, ndi osauka, ndipo sakudziwa izo.”

<sup>157</sup> Mulungu, chitirani chifundo usikuuno, kwa iwo omwe akukweza dzanja lawo, iwo amene akulolera kuti Mzimu Woyera ulowemo. Mulole Iye adze, atsike ndi mitsinje ya madalitso Ake tsopano, ikutsanulira mu mtima uliwonse, ndi kuwasefukiritsa iwo ku-, chimwemwe chosofukira, kuti iwo akhoze kudziwa kuti Iye alimoyo. Apatseni iwo kumvetsa kwa momwe angakulandirireni Inu. Apatseni iwo kumvetsa kuti Inu muli pamenepo, wofunitsitsa kuti mulowe mu mtima mwawo kuposa momwe iwo aliri kuti akhale ndi Inu.

<sup>158</sup> Mulole kumverera kwachirendo kulikonse, chiwanda chirichonse chimene chakhala pozungulira, chikuwopyeza, “Tsopano, iwe suulandira Iwo. Iwe suulandira Iwo.” Mulole iwo amutche mdierekezi uyo “wabodza.” Mulungu anapanga lonjezo, ndipo Mulungu asunga lonjezo Lake. Koma ife tingakhoze bwanji, pamene ife tonse tikhala okokedwa ngati kamba mu chigoba chake?

<sup>159</sup> Ine ndikupemphera, Mulungu, kuti Inu mulimasule gulu ili la anthu, ndipo muutumize kuno Mzimu Woyera kuchokera Kumwamba, ndi nkokomo wawukulu wamphamvu pa iwo. Mulole mitima yawo ikhale yotseguka tsopano. Ndipo ngati iwo angakhoze kokha kuulandira Mzimu Woyera, Ambuye, Iye alengeza kwa iwo kuti madalitso onse a Mulungu ali awo. Perekani izo, Atate, mu Dzina la Ambuye Yesu. Amenii.

<sup>160</sup> Kodi inu simukumukonda Iye? [Osonkhana ati, “Amenii.”—Mkonzi.] Inu mukukhulupirira kuti Ichi ndi Choonadi? [“Amenii.”] Ine sindiri mochuluka mlaliki wazamipingo. Ine . . . Koma chimene ine . . .

<sup>161</sup> Ngati ine ndingakhoze kokha kuzifotokoza zomwe ine ndikuziwona mu mtima mwanga! Ine ndikuyiwona nthawi yotsiriza. Ine ndikudziwa kuti Uthengawu ndi woona. Ngati ine ndikanati ndikhale ndikufa ora lino, Uthengawu uli woona. Mwaona? Ine ndikukhulupirira kuti maso a anthu, nthawi zambiri, ali akhungu. Koma, Mulungu ali wolungama, mu m’badwo uliwonse. Iye anamutumiza Nowa. Ndi angati anapulumutsidwa? Ndi angati anapulumutsidwa mu masiku a Loti? Yesu anati, “Chomwecho izo zidzakhala ziri mu kudza kwa Mwana wa munthu.” Ndithudi, onani, apang’ono okha. Koma Uthenga unkapitirirabe, chimodzimodzi basi.

<sup>162</sup> Tsopano mvetserani. Ndi angati akukhulupirira kuti Mulungu ali pano? Tiyeni tiwone dzanja lanu. Ndi angati akukhulupirira kuti Iye ali *Yehova-rafa*, “nsembe yoperekedwa ndi Ambuye”? Ndi angati akukhulupirira kuti Iye ndi *Yehova-yire*, “Ambuye yemwe amakuchizani inu”? [Osonkhana ati, “Amenii.”—Mkonzi.]



163 Mvetserani, abwenzi. Nthawi zochulukira kwambiri, utumiki wanga mu Amereka sunakhale uli wamphamvu kwambiri, chifukwa zikuwoneka ngati anthu ali o—osokonezeka kwambiri. Wina amaphunzitsa chinthu china, ndi wina china, mmalo mokhala pansu ndi kulitenga Baibulo ndi kumaliwerenga Ilo kwa inu, mwaona, ndi kumakhala okhutitsidwa ndi Mzimu Woyera. Tsopano, taonani. Inu simukusowa . . .

164 Inu mwaphunzitsidwa, “Anthu amaika manja pa inu.” Izo nzabwino.

165 Utumiki wanga ndi woti uzitsimikizira umboni wa Yesu Khristu kuti anawuka kwa akufa.

166 Tsopano, ena a inu mumaganiza kuti Izo zinali kuwerenga maganizo. Inu munalemba makalata anu kuno lero ndipo munanena chomwecho. Usiku watha, ine ndinawatenga anthu omwe anali ndi makadi a pemphero, ndipo ndinawabweza iwo, ndipo ndinangotenga iwo omwe anali opanda makadi a pemphero.

167 Amzanga, ndiroleni ine ndinene kwa inu, ngati wantchito wa Khristu. Pano pali Gene ndi Leo, mzanga wa pachifuwa. Pano pali Dr. Vayle. Mwana wanga, Billy. Uko kuli M'bale Sothmann, manenjira wachi Canada. M'bale, M'bale Norman, yemwe wakonzaka msonkhano uno kuno. Amuna ambiri. Imbirani ku mzinda wanga. Aimbireni ameya amu mzindawo, Bambo Hodenpehl. Aimbireni oweruza. Muimbire gulu la polisi. Mumuimbire Dr. Sam Adair, dotolo wamkulu Kummwera, chipatala chachikulu. Afunseni iwo mtundu wake ndi masomphenya omwe ali kuchitika. Afunseni iwo ngati ziri zooni.

168 Muimbireni Dr. Sam Adair, usikuuno, mumufunse iye zomwe amachita pamene iye afika pamalo ovuta. Iye amabwera ku nyumba kwanga, ndi kugwada pa maondo ake, ndipo apo iye amakhala pamaso pa Mulungu, iye ndi ine, mpaka Mulungu atasonyeza masomphenya. Ndipo mumufunse iye ngati nthawi imodzi zinayamba zalepherapo konse. Muimbireni iye, ndiripira ineyo.

169 Dr. Sam Adair ali ndi chipatala chachikulu uko. Mumufunse iye momwe iye anapezera konse chipatalacho uko. Pamene iye anali ku nyumba yanga uko, akulira, ndipo anati, “Mzindawu ukusowa chipatala.” Ndipo ine ndinamuza iye kumene komwe icho chikanati chidzamangidwe, ndipo iye akanadzachimanga icho. Anati, “Iwe—iwe sungakhoze kuwagula malo amenewo,” anati, “zaka twente-faifi kuyambira pano. Ziri mu mabwalo mu Boston.”

170 Ine ndinati, “PAKUTI ATERO AMBUYE. Iwo akhala ali anu maora twente-foro asanakwane.” Ine ndinati, “Inu mudzakakhala ndi chipatala uko, chidzamangidwa ndi njerwa

zofiira. Inu mudzakhala ndi chikwangwani pa chitseko, ndi zina zotero, ndi zonga choncho.”

Iye anati, “Billy, ine sindikanakukaikira iwe pa chirichonse, mwanawanga.”

Ine ndinati, “Ambuye achipereka icho kwa inu, adokotala.”

<sup>171</sup> Muimbireni iye, usikuuno, ndipo mumufunse iye zomwe zinachitika. Mmawa wotsatira iye anandiyimbira ine, anati, “Ine ndikuzizidwa pafupi kufa. Iwo angondiyimbira kumene ine. Ndipo chinachake chinachitika usiku watha, ndipo ife tagula kale malowo.”

<sup>172</sup> Mufunse za odwala omwe iye amawatumiza uko ali ndi khansara, itawadya, opanda chiyembekezo nkomwe. Ife nkumupempherera iye. Iwo amandithamangitsira ine ku chipatala. Ife timapita mu chipinda ndi kutseka chitseko. Ambuye amasonyeza masomphenya, mwina kungonena pamene iwo ati azipita kapena basi zomwe ziti zichitike. Mfuseni iye ngati zinayamba zalepherapo.

<sup>173</sup> Izi ndi zazing’ono chabe pano. Izi ndi . . . Izi ndi zochepesetsa zomwe ine ndinayamba ndazona konse zitachitidwapo mu uliwonse wa misonkhano yanga. Ndiko kulondola. Ine ndayesera chirichonse kuti ndichiswe chinthucho. Ine ndimabwera apo, ndipo inu mumaganiza, “makadi apempherowo.” Ine ndinawatembenuza makadi a pemphero mwanjira ina. Ine ndikuyesera chirichonse. Ine ndiri pano ngati wantchito wanu ndi m’bale wanu, zinthu izi pano.

<sup>174</sup> Pano pali Banks Wood wakhala muno penapake, wogulitsa mabuku wanga.

<sup>175</sup> Leo, Gene, pano pali anyamata awiri apa, mmodzi Mkatolika, ndi winayo ine sindikuganiza anali wa ku chirichonse. Pamene iwo anafika ku Hammond, Indiana, ndipo atawona Mzimu Woyera, mwa masauzande a anthu awo, ukuwatchula, zaka zingapo zapitazo. Mmodzi wa iwo anaweta ndevu zazikulu kwambiri. Iwo anadzipangira F.B.I. yao yao, kuti abwere uko ndi kudzawona ngati zinthu zimenezo ziri zolondola. Anabwera kunyumba kwanga, kumachita ngati ndi alaliki, ndi zina zotero. Ndipo Mzimu Woyera unapita apo pomwe ndipo unazitchula izo. Ndi awa, akhala pano tsopano. Mukuona?

Bwanji simukukhoza kupirira nazo Izi? Chavuta ndi chiani?

<sup>176</sup> Bambo Woods, ali muno penapake, anali kundiuza ine, ali pomwe pano. Kutali uko mu Louisiana, ine ndinamuwona iye akuvulala. Ndinamuimbira iye pa lamya, ndipo ndinamuza iye kuti asalalire. Tsiku lotsatiralo, iye anadula chala chake chachikulu. Iye bwenzi atadula nkono wake; Mzimu Woyera. Mausiku angapo apitawo, pamene ine ndinali mu Chicago, ine ndinamuwona iye pakati pa utsi, ndipo ndinamuza iye kuti akhale akusalalitsa. Iye akanati atenge chiphe cha nkala

apo pomwe. Ndipo anakalowa mu utsi wochuluka uwo, ndipo akanati afe apo pomwe.

<sup>177</sup> Mufunse momwe zinthu zimanenedweratu, masabata pambuyo pa masabata, ndi miyezi pambuyo pa mwezi, izo zisanati zichitike.

<sup>178</sup> Mtsogolomu, mu sabata, ine ndikusonyezani inu chomwe izi ziri. Ichi ndi chikhulupiriro chanu chomwe; ndipo ndi chifukwa chake zinthu sizingakhoze kumachitika. Ndi inuyo mumakoka kuchokera kwa Mzimu Woyera. A... Yesu sanamuwonere konse masomphenya mkaziyo. Chija chinali chikhulupiriro chake chimene chinamukhudza Iye. Ndi chifukwa chake Iye anafooka. Ndi chikhulupiriro chanu chimene chimachita izo, si changa. Ndi inuyo amene mukuzichita izo. Ndipo ngati inu muchotsa kumverera kwa chipukupuku uko pa inu, ndi kumukhulupirira Mulungu kwenikweni, chinthu ichi chifalikira nkukhala chitsitsimutso chimodzi chachikulu cha haleluya, ndipo opuwala, akhungu, osayenda, ndi chirichonse chidzachitika. Koma pamene inu mungokhala matalala, Iye angakhoze bwanji kuzichita izo?

<sup>179</sup> Ine ndimakhulupirira za kukhala wosamalitsa. Koma, si kuti kokha, kuti chinthu chosamalitsacho chimakupatsa iwe mzimu wa zamatsenga. Musati mudiuze ine. Ine ndaima pano tsopano. Ine ndikudziwa chimene ine ndikuchikamba. Mzimu Woyera uli mu chipinda chino kumene, pakali pano, umuchiritsa wina aliyense wa inu kumene pomwe inu mwakhalapo, ngati inu muti mukhulupirire izo. Iye anachita kale izo. Ndi angati akukhulupirira izo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Kodi inu mukukhulupirira izo? [“Ameni.”] Chabwino.

Ine ndiwona kuchuluka kwa momwe inu mukukhulupirira.

<sup>180</sup> Weramitsani mitu yanu mphindi yokha. Ikani dzanja lanu pa winawake pafupi ndi inu. Tsopano ingochokani ku zamatsenga zirizonse. Inu muli pansu pa ulamuliro wa Khristu. “Paliponse pamene awiri kapena atatu asonkhana mu Dzina Langa, Ine ndidzakhala ndiri pakati pawo.”

<sup>181</sup> Inu mukhoza kunditcha ine wachinyengo, koma inu muzipeza mu miniti. Ine ndikuwawona anthu pakali pano akuchiritsidwa, ndiko kulondola, pakali pano. Inu mukhoza kusachizindikira icho tsopano. Koma ngati azibusa mu chipinda chino sawawona anthu akubwera kwa iwo ine nditachoka kale, kudzawauza iwo kuti mavuto a mmimba ndi zinthu zonga izo zawachokera iwo, ndine mboni yabodza. Kulondola. Ndiko kulondola. Ine ndikuziwona izo. Ine ndikuzipenya izo tsopano, mu dziko lina.

<sup>182</sup> Inu mukhulupirire. Inu mukhulupirire. Ndithudi, ngati Nkafula mbuli yosawuka mu Afrika, yemwe samadziwa nkomwe lomwe liri dzanja lamanja kapena lamanzere, angakhoze kuzivomereza Izo, nanga bwanji inu omwe mungakhoze

kuwerenga Baibulo ndipo munaphunzitsidwa mu Chikhristu? Ngati munthu wosauka uyo angakhulupirire, kwa nthawi imodzi yokha pakuyang'ana pa Icho, chifukwadi ine ndikuyenera kuti ndipite kwinakwake tsiku lotsatira, ndipo masauzande akuuka kuchokera mzikuku, ndi olumala ndi akhungu, nanga bwanji inu?

<sup>183</sup> O Mulungu, momwe Inu muliri wachifundo, “Momwe muliri wopirira, wosalola kuti aliyense awonongeke.”

<sup>184</sup> Tsopano khalani, modzitsekera ndi Mulungu. Vomerezani tchimo lanu. Vomerezani kusakhulupirira kwanu. Muuzeni Mulungu mukudzichitira nokha manyazi, ndi kusakhulupirira kwanu. Ine ndikukutsutsani inu kuti muchite izo, ndipo inu muwona ulemmero wa Mulungu.

<sup>185</sup> Ine ndikumverera kudzozedwa pakali pano kuti ndichite chinachake chosiyana ndi momwe ine ndinayamba ndachitirapo. Ine sindinayambe ndachitapo izi, mu moyo wanga, koma ine ndikumverera kutsogozedwa kuti ndichite izo pakali pano.

<sup>186</sup> Vomerezani tchimo lanu pakali pano. Inu mukuti, “Chabwino, ndine Mkhristu.” Vomerezani kusakhulupirira kwanu. Mumuuzeni Khristu kuti simudzamukaikira konse Iye kachiwiri. Pakali pano inu mukumuvomereza Iye. Pakali pano izo zitha. Inu simudzadandaula konse za izo, kenanso. Ziribe kanthu momwe izo zikuwonekera, momwe izo zikumvereredwa, inu muziwakhulupirira Iwo, chifukwa Mulungu ananena chomwecho. Mulungu ananena chomwecho.

<sup>187</sup> Inu mwabwera kuchokera ku nsanja ya Babeloni. Inu mwabwera ku chigwa komwe Kakombo wa Mchigwa ali. Inu mwabwera kumbali ya phiri kumene chisomo cha Mulungu chikuyenderera mosavutikira kuchokera ku Kasupe wa Moyo.

<sup>188</sup> Vomerezani zolakwitsa zanu. Itini, “Mulungu . . .” Ngati inu munachita chirichonse kwa winawake, itini, “Ine ndibwerera ndi kukachikonza icho.” Chitani izo tsopano.

<sup>189</sup> Ine ndikufuna wina aliyense wa inu tsopano, pamene ine ndikunena pemphero ili, ine ndikufuna inu muzilipempherera ilo. Inu muzilinena ilo momveka, ndi ine. Ine ndikuti ndizingolinena ilo, koma inu muzipemphera ilo kuchokera mu mtima mwanu, ndi mutu wanu woweramitsidwa, maso atatekedwa, aliyense. Musati muutse mutu wanu mpaka ine nditanena chomwecho. Ine ndikungoyang'ana kuti ndiwone chimene ine ndingakhoze kuchiwona. Muzinena chonchi, mmbuyo mwanga.

<sup>190</sup> Mulungu Wamphamvuzonse, [Osonkhana ati, “Mulungu Wamphamvuzonse,”] Mlengi wa miyamba ndi dziko lapansi, [“Mlengi wa miyamba ndi dziko lapansi,”] Mwini wa Moyo wosatha, [“Mwini wa Moyo wosatha,”] Wopereka wa mphantho yabwino iliyonse, [“Wopereka wa mphantho yabwino iliyonse,”] ndichitireni chifundo ine, O Mulungu. [ndichitireni

chifundo ine, O Mulungu.”] Khululukirani kusakhulupirira kwanga. [“Khululukirani kusakhulupirira kwanga.”] Ine ndikuwukhulupirira Uthenga. [“Ine ndikuwukhulupirira Uthenga.”] Ine ndikukhulupirira kuti Inu muli pano. [“Ine ndikukhulupirira kuti Inu muli pano.”] Ine ndikukhulupirira kuti Inu tsopano mukuchita Mawu Anu [“Ine ndikukhulupirira kuti Inu tsopano mukuchita Mawu Anu”] mu thupi langa. [“mu thupi langa”] Tsegulani timipita. [“Tsegulani timipita.”] Ine ndikukhuthula kusakhulupirira kwanga. [“Ine ndikukhuthula kusakhulupirira kwanga.”] Ine ndikulandira Mzimu Wanu. [“Ine ndikulandira Mzimu Wanu.”] Ine ndikukhulupirira kuti Inu muli mwa ine tsopano. [“Ine ndikukhulupirira kuti Inu muli mwa ine tsopano.”] Ine ndikukhulupirira matenda anga achoka. [“Ine ndikukhulupirira matenda anga achoka.”] Zingakhoze bwanji imfa ndi moyo [“Zingakhoze bwanji imfa ndi moyo”] kukhala mu thupi langa [“kukhala mu thupi langa”] pamene Inu muli mmenemo? [“pamene Inu muli mmenemo?”] Ine ndikukukhulupirira Inu. [“Ine ndikukukhulupirira Inu.”] Ndipo ine ndikukuvomerani Inu tsopano [“Ndipo ine ndikukuvomerani Inu tsopano”] monga Mchiritsi wanga. [“monga Mchiritsi wanga.”—Mkonzi.]

Tsopano khalani mitu yanu ili chiweramire.

<sup>191</sup> Ndilo pemphero lanu. Ndilo pemphero lanu. Tsopano ine ndikuti ndikupempherereni inu. Khalani mutadzitsekera mkati. Khalani mutadzitsekera mkati ndi Mulungu. Musati mutenge china chirichonse kuchokera mu malingaliro anu tsopano. Iye ali ndi inu kumene, apo pomwe chapambali yanu. Inu mukuti, “Ine ndikufuna Mzimu Woyera, M’bale Branham.” Chabwino. Iye ali apo pomwe kuti awupereke Iwo. Inu mukuti, “Ine ndikufuna machiritso mu maso anga, M’bale Branham.” Iye ali apo pomwe kuti apereke izo. “Ine ndikufuna kuti mwana wanga achiritsidwe.” Iye ali apo pomwe kuti akuchitireni izo. “Ine ndikufuna m’bale wanga, amayi anga.” Iye ali apo pomwe kuti achite izo, apo pomwe. Yehova-yire, Nsembe yoperekedwa!

<sup>192</sup> Tsopano ine ndikuti ndikupempherereni inu. Baibulo linati, “Pemphero la chikhulupiriro lidzamupulumutsa wodwala. Mulungu adzawaukitsa iwo.” Ngati ine ndipeza chisomo pamaso panu, mwa kugwira ntchito kwa Mzimu Woyera, ine ndipemphera ndi mtima wanga wonse pakali pano kuti Mzimu Woyera uchitire umboni kwa inu kuti ntchitoyo ndi yotsirizidwa.

<sup>193</sup> O Mulungu, Atate anga, ine ndikudza mu Dzina la Yesu, kuti ndiwapempherere anthu awa omwe tsopano moona mtima ndi modzipereka avomereza zolakwitsa zawo. O Mulungu wodala, mulole uwu ukhale usiku umene iwo sadzawuiwala konse. Mulole Mzimu Woyera udze mu mtima uliwonse pakali pano ndipo ungosunthira kunja zonse, chirichonse, ndi matenda onse kuchokera mthupi lawo.

Ine tsopano ndikuchita makani naye Mdierekezi pa mtsutso.

<sup>194</sup> Satana, iwe ukudziwa kuti iwe wakwapulidwa. Iwe ulibe ufulu wovomerezeka. Yesu Khristu, Ambuye wanga, anakuvula iwe ulamuliro uliwonse umene unali nawo, pamene Iye anafa pa Kalvare kuti achotse tchimo ndi matenda. Ndipo sindiwe kanthu koma chonyengezera, ndipo ife tikuitanitsa kunyengezera kwakoko. Iwe ukudziwa kuti pamene Ambuye wathu anabwera ku mtengo, Iye anawutemberera mtengowo. Tsiku lotsatira iwo unali kufota. Ndipo Ambuye wathu anati kwa ophunzira Ake, ‘Khalani nacho chikhulupiriro mwa Mulungu. Pakuti ngati inu mudzanena, inu mukadzanena kwa phiri ili, ‘Sunthidwapo,’ osakaika mu mtima mwanu, koma kukhulupirira kuti zomwe inu mwanena zichitika, inu mukhoza kukhala nazo zomwe inu munanenazo.’

<sup>195</sup> Satana, iwe ukudziwa Lemba pa izo. Ndipo ine ndawaphunzitsa kumene anthu awa, kuti, Mulungu ali mwa iwo. Ndipo ngati Mulungu ali mwa iwo, ndipo iwo akayankhula kwa matenda awo ndi kuti, “Khala kutali ndi ine,” ndipo akapanda kukaika mu mtima mwawo, apo pomwe matenda awo ayenera kuti achokepo, chifukwa Khristu ananena chomwecho. Pakuti, si iwo omwe akuyankhula. Ndi Atate amene akukhala mwa iwo, omwe akuyankhula. Iwo ali ndi chosowa. Chotero, tuluka mwa iwo, mu Dzina la Yesu Khristu. Ine ndikunena, monga wantchito wa Mulungu, ndi Uthenga wochokera kwa Mngelo Yemwe anadzoza ndipo watsimikizira kwa anthu kuti Yesu ali pano ndipo Uthengawu ndi wolondola. Chotero, tuluka mwa iwo, mu Dzina la Yesu Khristu. Ine ndikukulumulira iwe kuti umusiye munthu wodwala aliyense ndipo upite ku mdima wakunja, mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu.

[Phokoso la Mphepo Yopatulika likumveka—Mkonzi.]

<sup>196</sup> Kodi inu munazimva Izo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi] Ine ndikutsimikiza inu munazimva Izo. Ndi angati anamwa Chiphokoso chachikulu chija chikudutsa mchipindamu posachedwapa? Icho chinali Iwo. Ndithudi inu simukaikira kenanso. Ameneyo anali Mulungu, akuyankhula moyankha. Kodi inu simungakhoze kuwona? [Osonkhana akusangalala.]

<sup>197</sup> Nyamukani. Kodi inu mukukhulupirira kuti mwachiritsidwa? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Kodi mukukhulupirira kuti Mulungu anayankha pemphero? Kwezerani manja anu kwa Iye. Muthokozeni Iye chifukwa cha izo. [Osonkhana akusangalala.] Izo zatha. Inu mwachiritsidwa.

<sup>198</sup> Yesu anati, “Ngati inu mudzanena.” Ndi chiani icho? Pamene inu mwatuluka kuchokera ku Babeloni, inu mwachoka pansu pa kusakhulupirira. Inu mwachoka pansu pa zamatsenga. Inu mwachoka pansu pa zinthu zonse izi. Ndipo inu mwadzazidwa ndi Moyo wa Mulungu Womwe. Liwu lanu ndi Liwu Lake. Inu muli.

199 Ine ndinachiyankhula icho. Mu chipinda changa, kanthawi kapitako, Mulungu anandiuza ine kuti ndichite izi. Ndipo pano Izo ziri. Iye wazitsimikizira izo pakali pano. [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Ameni. Ndipo lodala likhale Dzina la Ambuye. O, ndi nthawi bwanji! Ndi nthawi yoyamba yomwe Icho chachitika chichokereni ku South Afrika. Ndi motalika bwanji inu muti muziyenda mwa kusakhulupirira? Mwazimva izo? Mphepo inasesa kudutsa pa nsanja ino pomwe pano, pamene Mzimu Woyera umadutsa cha pano, chifukwa anali Mawu oyankhulidwa a Mulungu amene anachita izo. Ameni.

200 Ndi angati a inu mwachiritsidwa? Kwezani manja anu. Ndi angati mukumverera kusiyana mu thupi lanu? Kwezani dzanja lanu. [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Ndi izo apo. Inu mwachiritsidwa tsopano ndi ulemerero wa Mulungu. Onse amene akumverera mosiyana, ngati inu simumakhoza kuusuntha nkono wanu, usuntheni iwo. Ngati inu simumakhoza kumva kuchokera mu khutu lanu, tokosani chala chanu mu khutu ndipo mumvetsere. Inu mukukhoza kumva. Ngati inu simumakhoza kuyenda, imani pa mapazi anu. Ngati ndinu wakhungu, chotsani zotchinga zanu pa maso anu. Inu mukhoza kuwona.

201 Mzimu Woyera unadutsa pamalo ano posachedwapa mwa kutsimikizira kwa Mawu. Aleluya! Lidalitsike Dzina la Ambuye. Yokhala ngati Mphepo inadutsa mchipinda muno. Ndi angati anakhoza kuimverera Iyo pamene Iyo imadutsa muno? Kwezani dzanja lanu. Mukhale woonamtima ndi inueni. Mphepo ija yomwe inadutsa mu nyumba muno, ndiwo Mzimu Woyera. [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] “Muzinene izo, ndipo izo zichitidwa.” Monga Mphepo yaikulu yokondeka inapita “psfyuu,” pansi pomwepo kudutsa pano, ndipo ine ndinaimva Iyo pamane Iyo imadutsa mwa omvetsera. Inu munaimva Iyo ndipo munaimverera Iyo, inunso. Ndi Kukhalapo Kwake.

202 Onse tsopano omwe akumverera mosiyana, onse tsopano omwe akumverera kuti inu mwachiritsidwa, onse tsopano omwe mukumverera kuti Khristu ali mwa inu!

203 Chinali chiani Icho? Basi monga Mzimu Woyera unadza pa Tsiku la Pentekoste, unabwera pansi pomwe, Mphepo imene inasesa muno. Ndi angati ali mboni ya Izo? Kwezani dzanja lanu. Aliyense, moonamtima kuchokera mu mtima mwanu. Ndi awo apo. Iyo inasesa kumene kudutsa mchipinda chino apo. Ndi Mzimu Woyera womwewo. [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Mzimu Woyera womwewo ukudza mwa Mawu omwewo. Lidalitsike Dzina la Ambuye. Ameni.

204 Onse amene akukhulupirira kuti inu mwachiritsidwa, imani pa mapazi anu. Aliyense yemwe mukukhulupirira kuti mukumverera mosiyana, eya, kuti inu pakali pano mwachiritsidwa, imani pa mapazi anu. [Osonkhana

akusangalala—Mkonzi.] Ameni. Ameni. Ndi zimenezo. Ameni. Pamene iwo akuyembekezera, pamene inu mukuyamba kumverera mosiyana! Ngati inu munali ndi kupweteka kwa mutu, ngati iko kwachoka, imirirani. Ngati inu mumadwala mmimba mwanu, imirirani, ngati iko kwapita. Imirirani ngati mboni. Ndi inu apo. Ndi chiani chimene chikuchita izo? Ndi Mzimu Woyera umene unachita izo. Ameni. Kudzazidwa ndi ubwino Wake! O, mai!

<sup>205</sup> “Iyi ndi nkhani yanga, iyi ndi nyimbo yanga.” O, kodi inu simukumverera bwino? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.]

. . . -ni, iyi ndi nyimbo, (aliyense),  
Kumtama Mpulumutsi tsiku lonse;  
Iyi ndi nkhani, o, ndi nyimbo yanga,  
Kumtama Mpulumutsi tsiku lonse.

Tiyeni tiyiimbe iyo kachiwiri, aliyense. Itengeni iyo.

Iyi ndi nkhani, o, ndi nyimbo yanga, (aliyense),  
Kumtama Mpulumutsi tsiku lonse;  
Iyi ndi nkhani, o, ndi nyimbo yanga,  
Kumtama Mpulumutsi lonse. . .

<sup>206</sup> Kodi zimamverereka motani kukhala mutachiritsidwa? Gwedezerani manja anu kwa Iye, momwe zikumverereka kuti mwachiritsidwa. Tangoyang’anani apo. Mundiuze ine kuti Mdierokezi sunagonjetsedwe? Ndithudi, iye ali. Ameni. [Osonkhana akusangalala—Mkonzi.]

<sup>207</sup> Iye ndi wodabwitsa. O, mai! Tipatseni ife kayimbidwe kake, “Wodabwitsa, wodabwitsa, Yesu ali kwa ine.” Ndi angati akuidziwa nyimbo imeneyo?

Wodabwitsa, wodabwitsa, Yesu kwa ine,  
Wauphangu, Kalonga wa Mtendere, Mulungu  
Wamphamvu.

Chabwino. Mukuidziwa iyo, mlongo. Chabwino.

Wodabwitsa, wodabwitsa, Ye- . . .  
Wauphangu, Kalonga wa Mtendere, Mulungu  
Wamphamvu;

O, kundipulumutsa, kundisunga ku tchimo ndi  
manyazi,  
Wodabwitsa, Muomboli wanga, Mtame Dzina  
Lake!

O, wodabwitsa, wodabwitsa, Yesu kwa ine,  
O, Wauphangu, Kalonga wa mtendere,  
Mulungu Wamphamvu;

O, kundipulumutsa, kundisunga ku tchimo ndi  
manyazi,  
Wodabwitsa ndi Muomboli wanga, mtame. . .

<sup>208</sup> Kwa phindu, ngati pakanati pakhale wokaikira ataima cha pano, chimene, ine ndikuchimverera icho mu mtima mwanga



tsopano ndi motsutsa Mzimu wanga. Winawake akuganiza kuti Phokoso lija linadutsa pano nthawi ija linapangitsidwa ndi ndege kapena chinachake.

<sup>209</sup> Mulungu, Yemwe ali Woweruza wanga wakachetechete, Mzimu uja unabwera pa nsanja ino, mpaka unakupizira chikhotho changa pambali pa ine, ndi Kupokosera mu chipinda icho apo pomwe. Ine ndinaimverera Iyo, ndinaiwona Iyo, pamene Iyo imapita uko. Ndi angati ali mboni tsopano? Baibulo linati, “Pakamwa pa mboni ziwiri kapena zitatu.” [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Ndi mwamtheradi osati. . . Ndi Mzimu Woyera.

<sup>210</sup> Inu mukukumbukira pamene Yesu anali kupemphera, nthawi yina, ndipo apo panali Chipokoso chinabwera kuchokera Kumwamba? Ndi angati akuzikumbukira izo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Ndipo ena a iwo anati, o, chinachake, “kwabingula” kapena chinachake chonga icho. Uwo ukanali. Mzimu wokaikira ukadali moyo.

<sup>211</sup> Koma, Mulungu akadali wamoyo, nayenso. Iye ali pomwe pano. Mphepo yomweyo ya nkokomo yomwe inatsika kuchokera Kumwamba pa Tsiku la Pentekoste ili pomwe pano kuti ichitire umboni chinthu chomwecho kachiwiri. Mulungu Wamphamvuzonse ndi Woweruza wa zinthu zonse. Ameni.

<sup>212</sup> Kodi inu mukumukonda Iye? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Ambuye alemekezeke. Chabwino. Aliyense afikire ndi kugwirana chanza wina ndi mzake pamene ife tikuyimba *Wodabwitsa* kachiwiri. Inu Amethodisti ndi Abaptisti lingalirani bwino tsopano. Chabwino.

Wodabwitsa, . . .

O, tembenikirani mozungulira, gwiranani chanza ndi aliyense wokuyandikirani.

. . . ine,

Wauphungu, Kalonga wa Mtendere, Mulungu  
Wamphamvu Iye;

O, kundipulumutsa, kundisunga ku tchimo ndi  
manyazi;

O, wodabwitsa Muomboli wanga, mtame  
Dzina Lake!

<sup>213</sup> Ambuye alemekezeke. Kodi inu mukumverera bwino tsopano? [Osonkhana ati, “Ameni.”] Ponseponse, kukaikira konse kwapita? Gwedezerani manja anu kwa Iye. “Iko kwapita. Kukaikira konse kwapita.” [Osonkhana akusangalala—Mkonzi.] O, mai! Zodabwitsa! Zodabwitsa! Zabwino! “Kukaikira konse kwapita.”

Mulungu akudalitseni inu, Dr. Vayle



*UMODZI WA CHIYANJANO* CHA58-0128  
(The Oneness Of Unity)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham woperekedwa mu Chingerezi Lachiwiri usiku, Januwale 28, 1958, ku ku Hippodrome mu Waterloo, Iowa, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira uku kwa Chichewa kunadindidwa m'chaka cha 2006 ndi Voice of God Recordings:

CHICHEWA

©2006 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)